



Kupeza Choonadi Pophunzira Baibulo

Biblica® Tsekulani Mawu a Mulungu mu Chichewa Chalero™

Mwini © 2002, 2016 ndi Biblica, Inc.

“Biblica” ndilo dzina lodziwika la ntchitoyi ku United States limene linalembedsedwa ndi Biblica mwini.

Limagwiritsidwa ntchito ndi chilolezo.

Discover Chichewa. v6 - 2022 discoverapp.org

Kupeza choonadi pophuzira Baibulo

1. KUWERENGA MAWU

- Kuwerenga ndi kumvetsera mawu.
- Kubwereza kuwerenga ndi kumvetsera mawu mpaka aliyense atamvetsetsa.

2. KUFOTOKOZERA

- Kufunsa aliyense afotokozere m'mene wamvera mawuwo.

3. ZOYENERA KULINGALIRA

- Kodi mawu awa akundiphunzitsa chiyani za Mulungu?
- Kodi mawu awa akundiphunzitsa chiyani za anthu?
- Ngati mawu a Mulungu akulankhula ndi moyo wanga, ndidzanvera motani?
- Kodi ndikadziwitsa yani?
- Kodi mawu awa akuchokera pati?

4. KALONDOLONDO WA NTCHITO

- Kodi ndakwaniritsa chiyani msabatayi?
- Ndimavuto ati amene ndakumana nawo msabatayi?

5. KUBWEREZA

- Tikuchitapo chiyani pa ntchito yomwe tidagwira?

Phunziro 1

CHILENGEDWE: Mulungu alenga kumwamba ndi dziko lapansi

Genesis 1:1-25

Chiyambi cha Chilengedwe

1 Pachiyambi Mulungu analenga kumwamba ndi dziko lapansi. **2**Dziko lapansi linali losakonzedwa ndi lopanda kanthu. Mdima wandiweyani unakuta nyanja ndipo Mzimu wa Mulungu unkayendayenda pamwamba pa madziwo.

3Pamenepo Mulungu anati, “Kuwale” ndipo kunawaladi. **4**Mulungu anaona kuti kuwalako kunali bwino ndipo lye analekanitsa kuwala ndi mdima. **5**Mulungu anatcha kuwalako “usana” ndipo mdima anawutcha “usiku.” Ndipo panali madzulo ndiponso mmawa pa tsiku loyamba.

6Kenaka Mulungu anati, “Pakhale thambo pakati pa madzi kuti lilekanitse madzi a m’mwamba ndi madzi a pansi.” **7**Ndipo Mulungu anapanga thambo nalekanitsa madzi amene anali pansi ndi pamwamba pa thambo lija, ndipo zinachitikadi. **8**Mulungu anatcha thambo lija “kumwamba.” Ndipo panali madzulo ndiponso mmawa pa tsiku lachiwiri.

9Mulungu anati, “Madzi a pansi pa thambo asonkhane pa malo amodzi kuti mtunda uwoneke,” ndipo zinachitikadi. **10**Mulungu anawutcha mtundawo “dziko,” madzi osonkhana pamodziwo anawutcha “nyanja.” Ndipo Mulungu anaona kuti zinali bwino.

11Kenaka Mulungu anati, “Dziko libereke zomera zobala mbewu, mitengo yobala zipatso za mbewu, molingana ndi mitundu yake.” Ndipo zinachitikadi. **12**Dziko linabereka zomera zokhala ndi mbewu monga mwa mitundu yake ndi mitengo yokhala ndi zipatso za mbewu m’kati mwake monga mwa mitundu yake. Ndipo Mulungu anaona kuti zinali bwino. **13**Ndipo panali madzulo ndiponso mmawa pa tsiku lachitatu.

14Mulungu anati, “Pakhale zowunikira kuthambo kuti zilekanitse usana ndi usiku. Ndipo zimenezi zikhale zizindikiro zoonetsa nyengo, masiku ndi zaka; **15**zikhale kuthambo kuti ziwunikire pa dziko lapansi. Ndipo zinachitikadi.” **16**Mulungu anapanga zowunikira zazikulu ziwiri; chachikulu chilamulire usana ndi chaching’ono chilamulire usiku. lye anapanganso nyenyezi. **17**Mulungu anaziyika mlengalenga kuti ziziwunikira pa dziko lapansi, **18**kuti zilamulire usana ndi usiku, ndi kuti zilekanitse kuwala ndi mdima. Mulungu anaona kuti zinali bwino. **19**Ndipo panali madzulo ndiponso mmawa pa tsiku lachinayi.

20Mulungu anati, “M’madzi mukhale zamoyo zochuluka ndipo mbalame ziwuluke mlengalenga pamwamba pa dziko lapansi.” **21**Choncho Mulungu analenga zamoyo zikuluzikulu za m’nyanja ndi chamoyo chamtundu uliwonse chokhala m’madzi ndi mbalame iliyonse ya mapiko monga mwa mtundu wake. Mulungu anaona kuti zinali bwino. **22**Mulungu anazidalitsa nati, “Muswane, ndi kudzaza m’madzi a m’nyanja, ndipo mbalame zichuluke pa dziko lapansi.” **23**Ndipo panali madzulo ndiponso mmawa pa tsiku lachisanu.

24Kenaka Mulungu anati, “Dziko lapansi litulutse zolengedwa zamoyo monga mwa mitundu yawo: ziweto, zolengedwa zokwawa ndi nyama zakuthengo, iliyonse monga mwa mtundu wake.” Ndipo zinaterodi. **25**Mulungu anapanga nyama zakuthengo monga mwa mitundu yawo, nyama zoweta monga mwa mitundu yawo ndi nyama zokwawa monga mwa mitundu yawo. Ndipo Mulungu anaona kuti zinali bwino.

Phunziro 2

CHILENGEDWE: Mulungu alenga munthu

Genesis 2:4-24

Adamu ndi Hava

⁴Mbiri ya momwe kumwamba ndi dziko lapansi zinalengedwera pa tsiku lija Yehova Mulungu ankazilenga ndi iyi:

Yehova Mulungu atapanga dziko lapansi ndi kumwamba, ⁵zitsamba zinali zisanamere ndipo chomera chilichonse chinali chisanamerenso popeza Yehova Mulungu anali asanagwetse mvula pa dziko lapansi. Panalibe munthu wolima nthaka, ⁶koma kasupe ankatuluka m'nthaka ndi kuthirira pa dziko lonse. ⁷Tsono Yehova Mulungu anawumba munthu kuchokera ku dothi nawuziramo mpweya wamoyo m'mphuno mwake ndipo munthuyo anakhala wamoyo.

⁸Kenaka Yehova Mulungu anatekula munda wa Edeni chakummawa; kumeneko anayikako munthu amene anamupanga uja. ⁹Ndipo Yehova Mulungu anameretsa m'mundamo mitengo ya mitundu yonse. Inali mitengo yokongola ndi ya zipatso zokoma. Pakati pa munda uja panali mtengo wopatsa moyo ndi mtengo wopatsa nzeru zodziwitsa chabwino ndi choyipa.

¹⁰Mtsinje wothirira mundawo unkatuluka mu Edeni; kuchokera apo unkagawikana kukhala mitsinje inayi. ¹¹Dzina la mtsinje woyamba ndi Pisoni; uwu umazungulira dziko lonse la Havila, kumene kuli golide. ¹²(Golide wa ku dziko ili ndi wabwino. Kulinso miyala yokongola ya bedola ndi onikisi). ¹³Dzina la mtsinje wachiwiri ndi Gihoni; uwu umazungulira dziko lonse la Kusi. ¹⁴Dzina la mtsinje wachitatu ndi Tigirisi; umayenda chakummawa kwa Asiriya. Ndipo mtsinje wachinayi ndi Yufurate.

¹⁵Yehova Mulungu anatenga munthu uja ndi kumuyika m'munda wa Edeni kuti awulime ndi kuwusamalira. ¹⁶Ndipo Yehova Mulungu analamula munthu uja kuti, “Uzidya zipatso za mu mtengo wina uliwonse m'mundamu; ¹⁷koma usadye zipatso za mu mtengo wodziwitsa chabwino ndi choyipa, popeza ukadzadya za mu mtengowu udzafa ndithu.”

¹⁸Ndipo Yehova Mulungu anati, “Sibwino kuti munthu akhale yekha. Ndidzamupangira mnzake womuthandiza.”

¹⁹Kenaka Yehova Mulungu anawumba ndi dothi nyama zonse zakuthengo ndi mbalame zonse zamlengalenga. Ndipo lye anapita nazo kwa munthu uja kuti akazipatse mayina; ndipo dzina lililonse limene Adamu anapereka ku chamoyo chilichonse, lomwelo linakhala dzina lake. ²⁰Choncho Adamu anazitcha mayina ziweto zonse, mbalame zamlengalenga ndi nyama zakuthengo zonse.

Komabe munthu uja analibe mnzake womuthandiza. ²¹Tsono Yehova Mulungu anamugonetsa munthu uja tulo tofa nato; ali mtulo chomwecho, Mulungu anachotsa imodzi mwa nthiti zake ndi kutseka pamalopo ndi mnofu. ²²Motero Yehova Mulungu anapanga mkazi ndi nthiti ija imene anatenga kwa munthu uja nabwera naye kwa iye.

²³Munthu uja anati,

“Uyu ndiye fupa lochokera ku mafupa anga
ndi mnofu wochokera ku mnofu wanga;
adzatchedwa ‘mkazi,’
popeza wachokera mwa mwamuna.”

²⁴N'chifukwa chake, mwamuna amasiya abambo ndi amayi ake nakaphatikana ndi mkazi wake ndipo awiriwo amakhala thupi limodzi.

Phunziro 3

KUCHIMWA KWA MUNTHU: Kuchimwa koyamba ndi chilango chake

Genesis 3:1-24

Kuchimwa kwa Munthu

3 Ndipo njoka inali yochenjera kuposa nyama yakuthengo iliyonse imene Yehova Mulungu anapanga. Njokayo inati kwa mkaziyo, “Kodi Mulungu ananenadi kuti, ‘Inu musadye zipatso za mtengo uliwonse m’mundamu?’ ”

2Mkaziyo anati kwa njokayo, “Tikhoza kudya zipatso za m’mitengo ya m’mundawu, **3**koma Mulungu anati, ‘Musadye zipatso za mu mtengo umene uli pakati pa munda, ndipo musadzawukhudze kuti mungadzafe.’ ”

4“Ndithudi simudzafa,” inatero njokayo kwa mkaziyo. **5**“Pakuti Mulungu akudziwa kuti tsiku limene mudzadye zipatso za mu mtengowo, maso anu adzatsekuka, ndipo mudzakhala ngati Mulungu, wodziwa zabwino ndi zoyipa.”

6Pamene mkaziyo anaona kuti mtengowo unali wabwino kudya ndi wokongola ndi kuti unali wopatsa nzeru, anatengako zipatso zake nadya. Zina anamupatsako mwamuna wake amene anali naye pomwepo ndipo naye anadyanso. **7**Kenaka maso awo anatsekuka, ndipo anazindikira kuti anali maliseche. Choncho anasoka masamba a mkuyu nadzipangira zovala.

8Kenaka munthu uja ndi mkazi wake anamva mtswatswa wa Yehova Mulungu akuyendayenda m’mundamo madzulo a tsikulo, ndipo iwo anabisala pamaso pa Yehova Mulungu pakati pa mitengo ya m’mundamo. **9**Yehova Mulungu anayitana munthu uja kuti, “Uli kuti?”

10Iye anayankha, “Ndinakumvani m’mundamo, ndipo ndimaopa chifukwa ndinali maliseche; choncho ndinabisala.”

11Ndipo anamufunsa, “Ndani anakuwuzza kuti uli maliseche? Kodi wadya zipatso za mtengo umene ndinakulamulira kuti usadye?”

12Koma munthu uja anati, “Mkazi amene munandipatsa kuti ndizikhala nayeyu anandipatsako chipatso cha mtengowo ndipo ndinadya.”

13Tsono Yehova Mulungu anati kwa mkaziyo, “Wachitachi n’chiyani?”
Mkaziyo anati, “Njoka inandinamiza, ndipo ndinadya.”

14Choncho Yehova Mulungu anati kwa njokayo, “Popeza wachita zimenezi,
“Ndiwe wotembereredwa kuposa ziweto zonse
ndi nyama zakuthengo zonse.

Udzayenda chafufumimba
ndipo udzadya fumbi
masiku onse a moyo wako.

15Ndipo ndidzayika chidani
pakati pa iwe ndi mkaziyo,
pakati pa mbewu yako ndi mbewu yake;
Iye adzaphwanya mutu wako
ndipo iwe udzaluma chidendene chake.”

16Kwa mkaziyo Iye anati,
“Ndidzachelukitsa ululu wako kwambiri pamene uli ndi pakati;
ndipo udzamva ululu pa nthawi yako yobereka ana.

Udzakhumba mwamuna wako,
ndipo adzakulamulira.”

17Ndipo kwa Adamu Mulungu anati, “Chifukwa wamvera mkazi wako ndipo wadya zipatso za mu mtengo umene ndinakulamulira kuti, ‘Usadye.’

“Nthaka yatembereredwa chifukwa cha iwe,
movutikira udzadya zochokera m’nthakamo

masiku onse a moyo wako.

¹⁸M'nthakamo mudzamera minga ndi nthula
ndipo udzadya zomera zakuthengo.

¹⁹Kuti upeze chakudya udzayenera
kukhetsa thukuta,
mpaka utabwerera ku nthaka
pakuti unachokera kumeneko;
pakuti ndiwe fumbi
ku fumbi komweko udzabwerera.”

²⁰Munthu uja anatcha mkazi wake Hava, chifukwa iyeyu adzakhala mayi wa anthu onse amoyo.

²¹Yehova Mulungu anapangira Adamu ndi mkazi wake zovala zachikopa ndipo anawaveka. ²²Ndipo Yehova Mulungu anati, “Tsopano munthu uyu wasanduka mmodzi wa ife, wodziwa zabwino ndi zoyipa. Iyeyu asaloledwe kutambasula dzanja ndi kutengako zipatso za mu mtengo wopatsa moyo uja kuti angakhale ndi moyo mpaka muyaya.” ²³Kotero Yehova Mulungu anatulutsa Adamu M'munda wa Edeni kuti azilima m'nthaka imene anachokera. ²⁴Atamuthamangitsa munthu uja, Yehova anayika Akerubi mbali ya kummawa kwa Munda wa Edeni ndi lupanga lamoto limene limayendayenda ponsepo, kuteteza njira ya ku mtengo wopatsa moyo.

Phunziro 4

KUCHIMWA KWA MUNTHU: Chigumula cha Nowa

Genesis 6:1-9:17

Kuyipa kwa Mtundu wa Anthu

⁶ Anthu atayamba kuchuluka pa dziko lapansi ndi kubereka ana aakazi, ² ana aamuna a Mulungu anaona kuti ana aakazi a anthuwo anali okongola. Ndipo anakwatira aliyense amene anamusankha. ³ Tsono Yehova anati, “Sindilola kuti chipwirikiti chikuchitikachi chipitirire mpaka muyaya, pakuti iye ndi munthu; masiku a moyo wake adzakhala zaka 120.”

⁴ Masiku amenewo komanso pambuyo pake, pa dziko lapansi panali Anefili, anthu amphamvu ndiponso otchuka. Anthuwa ndi amene ankabadwa ana a Mulungu aja atakwatira ana aakazi a anthu.

⁵ Pamene Yehova anaona kuti kuyipa kwa munthu pa dziko lapansi kunali kwakukulu ndi kuti nthawi zonse amalingalira ndi kukumbira kuchita zoyipa zokhazokha, ⁶ Yehova anamva chisoni kuti analenga munthu ndi kumuyika pa dziko lapansi, ndipo anawawidwa mtima. ⁷ Choncho Yehova anati, “Ndidzafafaniza munthu, nyama, zonse zokwawa, ndi mbalame za mu mlengalenga pa dziko lapansi, pakuti ndikumva chisoni kuti ndinazilenga zimenezi.” ⁸ Koma Yehova anamukomera mtima Nowa.

Nowa ndi Chigumula

⁹ Mbiri ya Nowa inali yotere:

Nowa anali munthu wolungama ndi wopanda tchimo pakati pa anthu a m'bado wake. Ndipo anayenda ndi Mulungu. ¹⁰ Nowa anabereka ana aamuna atatu: Semu, Hamu ndi Yafeti.

¹¹ Chiwawa chinadzaza pa dziko lapansi kotero kuti dziko linakhala lowonongeka pamaso pa Mulungu. ¹² Mulungu atayang'ana, anaona kuti dziko layipadi chifukwa cha makhalidwe oyipa a anthu onse pa dziko lapansi. ¹³ Ndipo Mulungu anati kwa Nowa, “Ndatsimikiza mtima kuti ndiwononge anthu onse, pakuti dziko lapansi ladzaza ndi ntchito zawo zoyipa. Ndithudi ndiwawononga pamodzi ndi zonse za pa dziko. ¹⁴ Tsono udzipangire chombo cha matabwa a mtengo wanjale; m'kati mwake upange zipinda ndipo upake phula m'kati ndi kunja. ¹⁵ Uchipange motere: Chombo chikhale mamita 140 mulitali, mamita 23 mulifupi ndi mamita 13 mu msinkhu wake. ¹⁶ Uchipangire denga ndi kuchimaliza ndi zenera la masentimita makumi asanu. Uyike khomo m'mbali mwa chombocho ndi kupanga zipinda zosanjikana; chapansi, chapakati ndi chapamwamba. ¹⁷ Ndidzagwetsa mvula ya chigumula pa dziko lapansi kuti ndiwononge zamoyo zonse za pansu pa thambo ndipo chilichonse cha pa dziko lapansi chidzafa. ¹⁸ Koma ndidzachita pangano langa ndi iwe. Iwe, ana ako aamuna, mkazi wako ndi akazi a ana ako nonse mudzalowa m'chombocho. ¹⁹ Iwe udzalowa m'chombocho ndi zolengedwa zamoyo zonse ziwiriziwiri, chachimuna ndi chachikazi, kuti zisungike ndi moyo pamodzi ndi iwe. ²⁰ Udzatenga ziwiriziwiri za mitundu yonse ya mbalame, mitundu yonse ya nyama, ndi mitundu yonse ya zokwawa kuti zikhale ndi moyo. ²¹ Udzatengenso chakudya cha mtundu uliwonse ndi kuchisunga kuti inu ndi nyamazo muzidzadya.”

²² Nowa anachita zonse monga Mulungu anamulamulira.

⁷ Ndipo Yehova anati kwa Nowa, “Lowa mu chombo iwe ndi banja lako lonse, chifukwa ndaona kuti ndiwe wolungama mu m'bado uwu. ² Pa mtundu uliwonse wa nyama zoti n'kudya utengepo zazimuna zisanu ndi ziwiri ndi zazikazi zisanu ndi ziwirinso. Koma pa mtundu wa nyama iliyonse yosati n'kudya utengepo zazimuna ziwiri ndi zazikazi ziwirinso. ³ Chimodzimidzinso mbalame, utenge zisanu ndi ziwiri zazimuna ndi zisanu ndi ziwiri zazikazi za mtundu uliwonse kuti mitundu yawo isungike ndi moyo pa dziko lonse lapansi. ⁴ Pakapita masiku asanu ndi awiri ndidzagwetsa mvula pa dziko lapansi kwa masiku makumi anayi usana ndi usiku ndipo ndidzawononga cha moyo chilichonse chimene ndinachipanga pa dziko lapansi.”

⁵Ndipo Nowa anachita zonse zimene Yehova anamulamulira.

⁶Pamene chigumula chinabwera pa dziko lapansi Nowa anali ndi zaka 600. ⁷Ndipo Nowa, ana ake aamuna, mkazi wake, pamodzi ndi ana ake aakazi analowa mu chombo chija kuthawa madzi a chigumula. ⁸Nyama zoti n’kudya ndi nyama zosadyedwa, mbalame, pamodzi ndi nyama zokwawa zonse zinadza kwa Nowa ziwiriziwiri ndi kulowa m’chombomo. ⁹Ndipo Nowa anatenga ziwiriziwiri, yayimuna ndi yayikazi monga anamulamulira Mulungu. ¹⁰Patapita masiku asanu ndi awiri chigumula chinabwera pa dziko lapansi.

¹¹Pa tsiku la 17 la mwezi wachiwiri, Nowa ali ndi zaka 600, akasupe onse akuya kwambiri anasefuka ndiponso zitseko za madzi akumwamba zinatsekuka. ¹²Ndipo mvula inagwa pa dziko lapansi masiku makumi anayi usana ndi usiku.

¹³Linali tsiku lomwelo pamene Nowa ndi ana ake aamuna, Semu, Hamu ndi Yafeti, pamodzi ndi mkazi wake ndi akazi a ana ake atatu aja analowa mu chombo. ¹⁴Iwowa analowa m’chombomo pamodzi ndi nyama iliyonse ya kutchire monga mwa mtundu wake, ziweto zonse monga mwa mitundu yawo, nyama yokwawa iliyonse monga mwa mtundu wake ndi mbalame iliyonse monga mwa mtundu wake. ¹⁵Nowa analowa mu chombo muja pamodzi ndi zamoyo zonse. ¹⁶Iye analowa nazo zazimuna ndi zazikazi monga mmene Mulungu anamulamulira. Kenaka Yehova anatseka pa khomo.

¹⁷Chigumula chinagwa pa dziko la pansu kwa masiku makumi anayi. Madzi anayamba kuchuluka ndipo ananyamula chombo chija ndi kuchiyandamitsa pamwamba pa dziko. ¹⁸Madzi anafika mwamphamvu ndipo anachulukirachulukira pa dziko lapansi moti chombo chinayandama pamwamba pa madziwo. ¹⁹Madzi a chigumula anabwerabe molimbika motero kuti mapiri ataliatali onse a pa dziko anamizidwa. ²⁰Madzi anakwera namiza mapiri kwa mamita pafupifupi asanu ndi awiri. ²¹Chamoyo chilichonse choyenda pa dziko lapansi chinafa: mbalame, ziweto, nyama zakuthengo, miyandamiyanda ya zonse zolengedwa za pa dziko lapansi pamodzi ndi anthu. ²²Chilichonse chamoyo, chokhala pa mtunda chinafa. ²³Chamoyo chilichonse pa dziko lapansi chinawonongedwa, kuyambira munthu, nyama, zokwawa ndi mbalame. Nowa yekha ndiye anatsala pamodzi ndi onse amene anali naye.

²⁴Madziwo anadzaza dziko lonse lapansi kwa masiku 150.

Nowa Atuluka M’chombo

¹Tsono Mulungu anakumbukira Nowa ndi nyama zonse zakuthengo ndi ziweto zimene anali nazo mu chombo. Yehova anatumiza mphepo pa dziko lapansi ndipo madzi anaphwera. ²Tsono akasupe a madzi ambiri a pansu pa dziko ndi zitseko za madzi a kumwamba zinatsekedwa, ndipo mvula inaleka kugwa. ³Madzi amaphwabe pa dziko lapansi. Pakutha pa masiku 150, madzi anatsika, ⁴ndipo pa tsiku la 17 la mwezi wachisanu ndi chiwiri, chombo chija chinakakhazikika pa mapiri a Ararati. ⁵Madzi anapitirira kuphwa mpaka mwezi wa khumi, ndipo pa tsiku loyamba la mwezi wa khumiwo msonga za mapiri zinayamba kuonekera.

⁶Patapita masiku makumi anayi, Nowa anatsekula zenera limene anapanga m’chombomo ⁷natulutsa khwangwala, koma khwangwalayo ankangowuluka uku ndi uku mpaka madzi anawuma pa dziko lapansi. ⁸Kenaka anatulutsa nkhunda kuti aone ngati madzi aphwa pa dziko. ⁹Koma nkhunda sinapeze poti n’kuterera chifukwa panali madzi ponseponse pa dziko lapansi. Choncho inabwerera kwa Nowa m’chombo. Nowa anatulutsa dzanja lake kunja ndi kutenga nkhundayo kuyibwezera m’chombo mmene iye anali. ¹⁰Choncho anadikirabe masiku ena asanu ndi awiri ndipo anatulutsanso nkhundayo m’chombo muja. ¹¹Pamene nkhunda inabwerera madzulo ake, inali itanyamula tsamba laliwisi la mtengo wa olivi. Motero Nowa anadziwa kuti madzi aphwadi pa dziko lapansi. ¹²Iye anadikira masiku ena asanu ndi awiri ndipo anatumizanso nkhunda ija, koma nthawi imeneyi sinabwererensu kwa iye.

¹³Pofika tsiku loyamba la mwezi woyamba wa chaka chimene Nowa anakwanitsa zaka 601, madzi anawuma pa dziko lapansi. Ndipo Nowa anachotsa denga la chombo ndipo anaona kuti kunja kwawuma. ¹⁴Pokwana tsiku la 27 la mwezi wachiwiri dziko lapansi linawumiratu.

¹⁵Tsono Mulungu anawuza Nowa kuti, ¹⁶“Iwe, mkazi wako, ana ako pamodzi ndi akazi awo tulukani m’chombomo. ¹⁷Tulutsa zamoyo zonse zili ndi iwe, mbalame, nyama ndi zokwawa zonse kuti ziswane ndi kuchulukana pa dziko lapansi.”

¹⁸Nowa anatuluka pamodzi ndi ana ake aamuna, mkazi wake ndi akazi a ana ake. ¹⁹Nyama zonse, zokwawa zonse, mbalame zonse, chilichonse choyenda pa dziko lapansi, zinatuluka m’chombo motsogozana monga mwa mitundu yawo.

²⁰Pamenepo Nowa anamanga guwa lansembe la Yehova ndipo anatengako mtundu uliwonse wa nyama zoti n’kudya ndi mbalame zoti n’kudya naperekapo nsembe yopsereza. ²¹Yehova atamva fungo labwino anati mu mtima mwake: “Sindidzatemberanso nthaka chifukwa cha munthu, ngakhale kuti maganizo a mu mtima mwake ndi oyipa kuyambira ubwana wake. Ndipo sindidzawononganso zolengedwa zonse zamoyo monga ndachitiramu.

²²“Nthawi zonse mmene dziko lapansi lidzakhalire,
nthawi yodzala ndi nthawi yokolola
yozizira ndi yotentha,
dzinja ndi chilimwe,
usana ndi usiku,
sizidzatha.”

Pangano la Mulungu ndi Nowa

⁹ Ndipo Mulungu anadalitsa Nowa ndi ana ake aamuna nati kwa iwo, “Berekanani ndipo muchulukane ndi kudzaza dziko lapansi. ²Nyama zonse za dziko lapansi, ndi mbalame zonse za mlengalenga, ndi chamoyo chilichonse chokwawa, ndiponso nsomba zonse za ku nyanja; zidzakuopani ndipo ndazipereka kuti muzilamulire. ³Tsopano chamoyo chilichonse chidzakhala chakudya chanu. Monga momwe ndinakupatsirani ndiwo zamasamba, tsopano ndikupatsaninso nyama iliyonse.

⁴“Koma musamadye nyama imene ikanali ndi magari oyenda. ⁵Aliyense wopha munthu adzaphedwa, nyama iliyonse yopha munthu idzaphedwa, munthu aliyense wopha munthu mnzake, adzaphedwa.

⁶“Aliyense wopha munthu,
adzaphedwanso ndi munthu;
pakuti Mulungu analenga munthu
m’chifanizo chake.

⁷Inu muberekane ndi kuchulukana kuti mudzaze dziko lonse lapansi ndi kuligonjetsa.”

⁸Mulungu anawuza Nowa ndi ana ake kuti, ⁹“Tsopano lne ndapangana ndi iwe ndi zidzukulula zako zam’tsogolomo, ¹⁰pamodzi ndi zamoyo zonse, mbalame, ziweto ndi nyama zonse za kuthengo, ndi zonse zimene zinatuluka m’chombo pamodzi ndi iwe. ¹¹Pangano langa ndi ili: lne ndilonjeza kuti sindidzawononganso zamoyo ndi madzi a chigumula. Chigumula sichidzawononganso dziko lapansi.”

¹²Ndipo Mulungu anati, “lne ndikupereka chizindikiro ichi cha pangano langa la pakati pa lne ndi iwe, ana ako, zamoyo zonse, pamodzi ndi mibado ya m’tsogolo. ¹³Ndayika utawaleza wanga m’mitambo, ndipo chidzakhala chizindikiro cha pangano langa ndi dziko lapansi. ¹⁴Nthawi zonse pakakhala mitambo mu mlengalenga ndipo utawaleza uwoneka, ¹⁵ndizikumbukira pangano langa pakati pa lne ndi inu ndi zolengedwa zonse. Madzi sadzakhanso chigumula chowononga dziko lapansi. ¹⁶Utawaleza ukamadzaoneka m’mitambo, ndidzawuona ndi kukumbukira pangano losatha pakati pa Mulungu ndi zamoyo zonse pa dziko lapansi.”

¹⁷Choncho Mulungu anati kwa Nowa, “Ichi ndiye chizindikiro cha pangano limene ndalichita pakati pa lne ndi zamoyo zonse pa dziko lapansi.”

Phunziro 5

CHIWOBOLO: Mulungu apangana ndi Abrahamu

Genesis 12:1-8, 15:1-6

Mulungu Ayitana Abram

12 Tsiku lina Yehova anamuwuzira Abram kuti, “Tuluka m’dziko lako. Siya abale ako ndi banja la abambo ako ndipo pita ku dziko limene ndidzakusonyeza.

²“Ndidzakusandutsa kholo la mtundu waukulu wa anthu ndipo ndidzakudalitsa;

ndi kukusandutsa wotchuka kotero kuti udzakhala dalitso kwa anthu ambiri.

³Ndidzadalitsa amene adzadalitsa iwe, ndi kutemberera amene adzatemberera iwe; ndipo mafuko onse a pa dziko lapansi adzadalitsika kudzera mwa iwe.”

⁴Choncho Abram ananyamuka monga momwe Yehova anamuwuzira, napita pamodzi ndi Loti. Pamene Abram amachoka ku Harani n’kuti ali ndi zaka 75. ⁵Abram anatenga mkazi wake Sarai, Loti, mwana wamng’ono wake, pamodzi ndi chuma chawo chimene anapeza ndi antchito amene anali nawo ku Harani. Iwo ananyamuka ulendo mpaka kukafika ku dziko la Kanaani.

⁶Abram anadutsa m’dzikomo mpaka kukafika ku Sekemu pa mtengo wa thundu wa ku More. Nthawi imeneyo Akanaani analipobe m’dzikomo. ⁷Yehova anadza kwa Abram nati, “Kwa zidzukuluzi zako ndidzapereka dziko limeneli.” Choncho Abram anamangira Yehova amene anadza kwa iye, guwa lansembe.

⁸Atachoka pamenepo analowera cha ku mapiri a kummawa kwa Beteli namangako tenti yake pakati pa Beteli chakumadzulo ndi Ai chakummawa. Kumeneko anamangira Yehova guwa lansembe napemphera m’dzina la Yehovayo.

Pangano la Mulungu ndi Abram

15 Zitatha izi, Yehova anayankhula ndi Abram m’masomphenya nati:

“Usaope Abram.

Ine ndili ngati chishango chokutchinjiriza.

Mphotho yako idzakhala yayikulu.”

²Koma Abram anati, “Haa! Ambuye Yehova, mukhoza kundipatsa chiyani popeza ndikanali wopanda mwana ndipo amene adzatenge chuma changa ndi Eliezara wa ku Damasiko? ³Inu simunandipatse ana kotero kuti wantchito wa ku nyumba kwanga ndiye amene adzalowe m’malo mwanga.”

⁴Yehova anayankhula naye nati: “Munthu uyu sadzalowa m’malo mwako, koma mwana wako weniweni wamwamuna, wobereka wekha ndiye adzalowe m’malo mwako.” ⁵Yehova anapita naye Abram panja nati, “Tayang’ana kumwambaku, ndipo chifukwa cha chimenechi uwerenge nyenyezi ngati ungathe kuziwerenga.” Ndipo anamuwuzira kuti, “Ndi mmene adzakhali ana ako ndi zidzukuluzi zako.”

⁶Abram anakhulupirira Yehova, ndipo ichi chinamuchititsa kukhala wolungama.

Phunziro 6

CHIWOBOLO: Abrahamu apeleka msembe

Genesis 22:1-19

Kuyesedwa kwa Abrahamu

22 Nthawi ina zitatha izi, Mulungu anamuyesa Abrahamu. Iye anati, “Abrahamu!”

Ndipo iye anayankha kuti, “Ee Ambuye.”

2 Ndipo Mulungu anati, “Tenga Isake, mwana wako yekhayo amene umamukonda ndi kupita naye ku dziko la Moriya. Ukamupereke iye ngati nsembe yopsereza pa limodzi la mapiri a kumeneko limene ndidzakuwuzwa.”

3 Abrahamu anadzuka mmamawa wake namangirira chokhalira pa bulu. Atadula nkhuhi zokwanira zowotchera nsembe yopsereza, Abrahamu, antchito ake awiri pamodzi ndi Isake ananyamuka kupita kumalo kumene Mulungu anamuwuzwa Abrahamu. **4** Pa tsiku lachitatu, Abrahamu anakweza maso ake ndipo anaona malowo chapatali. **5** Ndipo Abrahamu anati kwa antchito ake aja, “Bakhalani pano ndi buluyu. Ine ndi mnyamatayu tipita uko kukapemphera, koma tibweranso.”

6 Abrahamu anatenga nkhuhi za nsembe yopsereza zija namusenzetsa mwana wake Isake, ndipo iye mwini anatenga moto ndi mpeni. Pamene awiriwo amayendera pamodzi, **7** Isake anati kwa abambo ake Abrahamu, “Abambo?”

Abrahamu anayankha, “Ee mwana wanga.”

Isake anafunsa, “Moto ndi nkhuhi zilipo, koma nanga mwana wankhosa wa nsembe yopsereza ali kuti?”

8 Abrahamu anayankha, “Mwana wanga, Mulungu adzipezera yekha mwana wankhosa wa nsembe yopsereza.” Ndipo awiriwo anapitiriza ulendo.

9 Atafika pamalo pamene Mulungu anamuwuzwa paja, Abrahamu anamangapo guwa lansembe nayika nkhuhi pamwamba pa guwapo. Kenaka anamumanga mwana wake Isake namugoneka paguwapo, pamwamba pa nkhuhi paja. **10** Kenaka Abrahamu anatambasula dzanja lake natenga mpeni kuti aphe mwana wake. **11** Koma mngelo wa Yehova anayitana Abrahamu kuchokera kumwamba nati, “Abrahamu! Abrahamu!”

Iye anayankha kuti, “Ee Ambuye.”

12 Mngeloyo anati, “Usatambasulire mwanayo dzanja lako kuti umuphe, pakuti tsopano ndadziwa kuti iwe umaopa Mulungu. Iwe sunandimane mwana wako mmodzi yekhayo.”

13 Abrahamu anatukula maso ake ndipo anaona nkhosa yamphongo itakoledwa ndi nyanga zake mu ziyangoyango. Iye anapita nakatenga nkhosa ija ndikuyipha ngati nsembe yopsereza m’ malo mwa mwana wake. **14** Choncho Abrahamu anatcha malo amenewa kuti Yehova-Yire (Wopereka). Ndipo mpaka lero amatchula malowo kuti ndi “Pa phiri la Yehova wopereka.”

15 Mngelo wa Yehova anayitana Abrahamu kuchokera kumwamba kachiwiri **16** ndipo anati, “Ndikulumbira mwa Ine ndekha kuti popeza wachita zimenezi, wosandikaniza mwana wako mmodzi yekhayo, **17** ndidzakudalitsa ndithu ndipo ndidzakupatsa zidzukululu zochulukana ngati nyenyezi zamlengalenga komanso ngati mchenga wa m’mphepete mwa nyanja. Zidzukululu zako zidzalanda mizinda ya adani awo, **18** ndipo kudzera mwa chidzukululu chako, mitundu yonse ya anthu pa dziko lapansi idzadalitsika, chifukwa iwe wandimvera.”

19 Kenaka Abrahamu anabwerera kumene anasiya antchito ake kuja nanyamukira nawo pamodzi kupita ku Beeriseba. Ndipo Abrahamu anakhala ku Beeriseba.

Phunziro 7

CHIWOMBOLLO: Ionjezo la pasaka

Eksodo 12:1-28

Kukhazikitsidwa kwa Paska

12 Yehova anayankhula kwa Mose ndi Aaroni m'dziko la Igupto kuti, **2**“Mwezi uno uzikhala mwezi wanu woyamba wa chaka. **3**Muliwuze khamu lonse la Israeli kuti pa tsiku la khumi la mwezi uno, munthu aliyense asankhire banja lake mwana wankhosa mmodzi. Banja lililonse litenge mwana wankhosa mmodzi. **4**Ngati banja lili lochepa moti silingathe kudya nyama yonse ya nkhosa, ligawane ndi banja lomwe layandikana nalo nyumba. Mabanja adziwiretu chiwerengero cha anthu amene alipo pokonzekera zimenezi. Muwerengere kuchuluka kwa nyama imene anthu adzadye potengera mmene munthu mmodzi angadyere. **5**Ziweto zimene musankhe ziyenera kukhala zazimuna za chaka chimodzi, zopanda chilema, ndipo zikhale nkhosa kapena mbuzi. **6**Muzisunge mpaka tsiku la khumi ndi chinayi la mwezi, pamene gulu lonse la Israeli lidzaphe nyamazo madzulo. **7**Ndipo adzatengeko magazi anyamazo ndi kuwaza pa mphuthu ziwiri za chitseko ndiponso pamwamba pa chitseko cha nyumba mmene adzayeremo ana ankhosawo. **8**Adzawotche nyamayo ndi kudya usiku womwewo, ndipo adzayidye ndi buledi wophikidwa popanda yisiti pamodzi ndi masamba wowawa. **9**Musadzadye yayiwisi kapena yophika, koma mudzawotche yonse, mutu, miyendo ndi zam'mimba. **10**Musadzasiye nyama ina mpaka mmawa, ngati ina idzatsala mpaka mmawa, mudzayitenthe. **11**Muzidzadya nyamayo mutavala chotere, pokonzekera ulendo: mudzazimangirire lamba m'chiwuno, nsapato zanu kuphazi ndi ndodo yanu kumanja. Mudzadye mofulumira. Imeneyi ndi Paska ya Yehova.

12“Usiku umenewo Ine ndidzadutsa m'dziko la Igupto ndipo ndidzapha chilichonse choyamba kubadwa kuyambira mwana wa munthu aliyense mpaka ana aziweto. Ndidzalanganso milungu yonse ya Igupto. Ine ndine Yehova. **13**Magazi amene mudzawaze pa mphuthu za zitseko ndi pamwamba pa zitseko aja adzakhala ngati chizindikiro. Ine ndikadzaona magaziwo ndidzakudutsani, ndipo ndikadzamakantha anthu a Igupto, mliri wosakazawu sudzakukhudzani.

14“Ili ndi tsiku la chikumbutso. Tsiku limeneli muzidzachita chikondwerero, kupembedza Yehova. Mibado yonse imene ikubwera izidzakumbukira tsiku limeneli ngati lamulo lamuyaya ndi kuti pa tsikuli azidzachita chikondwerero cholemekeza Yehova. **15**Kwa masiku asanu ndi awiri muzidya buledi wopanda yisiti. Tsiku loyamba muzichotsa yisiti m'nyumba zanu, ngati aliyense adzadya kanthu kalikonse kali ndi yisiti kuyambira tsiku loyamba mpaka tsiku lachisanu ndi chiwiri, munthu ameneyo adzayera kuchotsedwa m'gulu la Israeli. **16**Pa tsiku loyamba muzichita msonkhano wopatulika, ndipo winanso uzikhala pa tsiku lachisanu ndi chiwiri. Musamagwire ntchito masiku onsewa, koma ntchito yokonza chakudya yokha kuti aliyense adye. Izi ndi zimene muzichita.

17“Muzichita chikondwerero cha buledi wopanda yisiti, chifukwa ndi pa tsiku limeneli ndinatulutsa magulu anu m'dziko la Igupto. Muzikondwerera tsiku limeneli pa mibado yonse ngati lamulo lamuyaya. **18**Mwezi woyamba muzidzadya buledi wopanda yisiti kuyambira madzulo tsiku la 14 la mweziwo mpaka tsiku la 21 mwezi womwewo. **19**Yisiti asamapezeka m'nyumba zanu kwa masiku asanu ndi awiri. Ndipo aliyense amene adya chakudya chimene muli yisiti, munthu ameneyo ayenera kuchotsedwa m'gulu la Israeli, kaya iyeyo ndi mlendo kapena mbadwa. **20**Musadye chilichonse chokhala ndi yisiti. Kulikonse kumene mukukhala, muyenera kudya buledi wopanda yisiti.”

21Ndipo Mose anasonkhanitsa akuluakulu onse a Israeli nati, “Pitani msanga kukasankha nkhosa zokwanira pa mabanja anu, ndipo muziphe ngati Paska. **22**Mutengenso nthambi ya chitsamba cha hisope, muchiviyike m'magazi amene mwawayika m'beseni ndipo muwaze ena mwa magaziwo pamwamba ndi m'mbali mwa mphuthu za chitseko. Palibe aliyense wa inu amene adzatuluke m'nyumba yake mpaka mmawa. **23**Pamene Yehova adzadutsa m'dziko kudzakantha Aigupto, n'kuona magazi pamwamba ndi m'mbali mwa mphuthu za chitseko, Iye

adzadutsa khomo limenelo ndipo sadzalola woonongayo kuti alowe m'nyumba zanu kuti akukantheni.

²⁴“Muzimvera malamulo amenewa kwa muyaya, inu ndi zidzukululu zanu. ²⁵Mukakalowa m'dziko limene Yehova adzakupatseni monga analonjeza, mukasunge mwambo umenewu. ²⁶Ndipo ana anu akakakufunsani kuti, 'Mwambo umenewu ukutanthauza chiyani?' ²⁷Inu mukawawuze kuti, 'Ndi nsembe ya Paska ya Yehova, popeza pamene ankakantha nyumba za Aigupto anasiya nyumba zathu.' ” Kenaka anthu anawerama napembedza. ²⁸Aisraeli anachita monga momwe Yehova analamulira Mose ndi Aaroni.

Phunziro 8

CHIWOBOLO: Malamulo khumi a Mulungu

Eksodo 20:1-21

Malamulo Khumi

20 Ndipo Mulungu anayankhula mawu onse awa nati:

3“Usakhale ndi milungu ina koma Ine ndekha.”

4“Usadzipangire chofanizira chinthu chilichonse chakumwamba kapena cha pa dziko lapansi kapena cha m’madzi a pansu pa dziko. 5Usazigwadire kapena kuzipembedza, pakuti Ine Yehova Mulungu wako, ndine Mulungu wansanje, wolanga ana chifukwa cha tchimo la makolo awo mpaka m’bado wachitatu ndi wachinayi wa iwo amene amadana nane. 6Koma ndimaonetsa chikondi chosasinthika ku mibado miyandamiyanda ya anthu amene amandikonda, ndi kusunga malamulo anga.

7“Usagwiritse ntchito molakwika dzina la Yehova Mulungu wako, pakuti Yehova adzamutenga kukhala wochimwa aliyense amene akugwiritsa ntchito dzina lakelo molakwika.

8“Uzisinga tsiku la Sabata kuti likhale lopatulika. 9Uzigwira ntchito zako zonse masiku asanu ndi limodzi. 10Koma tsiku lachisanu ndi chiwiri ndi Sabata, tsiku loperekedwa kwa Yehova Mulungu wako. Tsiku limeneli musagwire ntchito iliyonse, inuyo kapena mwana wanu wamwamuna kapena mwana wanu wamkazi, wantchito wanu wamwamuna kapena mdzakazi wanu, ziweto zanu kapena mlendo amene akukhala m’modzi mwanu. 11Pakuti Yehova anapanga kumwamba ndi dziko lapansi, nyanja ndi zonse zimene zili m’menemo m’masiku asanu ndi limodzi. Iye anapuma pa tsiku lachisanu ndi chiwiri. Kotero Yehova anadalitsa tsiku la Sabata kuti likhale loyera.

12“Lemekeza abambo ako ndi amayi ako kuti ukhale ndi moyo wautali m’dziko limene Yehova Mulungu wako akukupatsa.

13“Usaphe.

14“Usachite chigololo.

15“Usabe.

16“Usapereke umboni womunamizira mnzako.

17“Usasirire nyumba ya mnzako. Usasirire mkazi wa mnzako kapena wantchito wake wamwamuna kapena mdzakazi wake, ng’ombe yake kapena bulu wake, kapena chilichonse cha mnzako.”

18Pamene anthu ankamva mabingu ndi kuona ziphaliwali ndi kumvanso lipenga ndi kuona utsi umene umafuka m’phiri, ananjenjemera ndi mantha. Ndipo iwo anayima patali. 19Ndipo anati kwa Mose, “Iwe utiyankhule ndipo tidzamvera. Koma usalole kuti Mulungu atiyankhule, tingafe.”

20Koma Mose anati kwa anthuwo, “Musachite mantha. Mulungu wabwera kudzakuyesani kuti mukhale ndi mtima woopa Mulungu kuti musamuchimwire.”

21Anthu aja anayima patali koma Mose anayandikira mtambo wakuda kumene kunali Mulungu.

Phunziro 9

CHIWOBOLO: Lamulo lakupereka nsembe

Levitiko 4:1-35

Nsembe Yopepesera Tchimo

4 Yehova anayankhula ndi Mose kuti, 2“Awuze Aisraeli kuti, ‘Munthu akachimwa mosadziwa ndi kuchita chilichonse chimene Yehova walamula kuti asachite, azichita izi:

3“ ‘Ngati wansembe wodzozedwa achimwa, ndi kuchimwitsa anthu onse, iyeyu ayenera kupereka mwana wang’ombe wamphongo wopanda chilema chifukwa cha tchimo limene wachitalo. Imeneyi ndi nsembe ya Yehova yopepesera tchimo lake. 4Wansembeyo abwere nayo ng’ombeyo pa khomo la tenti ya msonkhano pamaso pa Yehova. Asanjike dzanja lake pamutu pa ng’ombeyo ndipo ayiphe pamaso pa Yehova. 5Kenaka wansembe wodzozedwa atengeko magazi a ng’ombeyo ndi kulowa nawo mu tenti ya msonkhano. 6Iye aviyike chala chake m’magazi, ndipo awawaze kasanu ndi kawiri pamaso pa Yehova, patsogolo pa katani yotchinga malo wopatulika. 7Kenaka wansembe apake magaziwo pa nyanga za guwa lofukizira lubani limene lili pamaso pa Yehova mu tenti ya msonkhano. Magazi ena otsalawo awathire pa tsinde pa guwa lansembe zopsereza, limene lili pa khomo la tenti ya msonkhano. 8Pambuyo pake achotse mafuta onse a ng’ombe yayimuna yopepesera machimoyo: mafuta okuta zam’kati kapena mafuta onse am’katimo. 9Achotsenso ndi kubwera ndi impyzo zonse ziwiri pamodzi ndi mafuta onse ndiponso mafuta onse amene aphimba chiwinda ndi impyzo 10monga momwe amachotsera mafuta a ng’ombe yoperekedwa kuti ikhale chopereka chachiyanjano. Tsono wansembe atenthe zimenezi pa guwa lansembe zopsereza. 11Koma chikopa cha ng’ombe yayimunayo ndi mnofu wake wonse, pamodzi ndi mutu ndi miyendo, zam’kati ndi matumbo, 12kapena kuti ng’ombe yonse yotsalayo apite nayo kunjwa kwa msasa ku malo woyeretsedwa, kumene amatayako phulusa ndi kuyitentha pa nkhu, pa phulusapo.

13“ ‘Ngati gulu lonse la Aisraeli lichimwa mosadziwa, nachita chomwe ndi choletsedwa ndi Yehova, ngakhale kuti gulu lonse silikudziwa kuti lachimwa, anthuwo ndi olakwa ndithu. 14Akazindikira tchimo limene achita, gulu lonse lipereke mwana wang’ombe wamphongo kuti akhale chopereka chopepesera tchimo ndipo abwere naye pa khomo la tenti ya msonkhano. 15Akuluakulu a anthuwo asanjike manja awo pa mutu pa ng’ombe pamaso pa Yehova, ndipo ayiphe pomwepo pamaso pa Yehova. 16Tsono wansembe wodzozedwa atengeko magazi a ng’ombeyo ndi kulowa nawo mu tenti ya msonkhano. 17Aviyike chala chake m’magaziwo ndi kuwawaza pamaso pa Yehova kasanu ndi kawiri patsogolo pa nsalu yotchinga. 18Pambuyo pake iye apake magaziwo pa nyanga za guwa limene lili pamaso pa Yehova mu tenti ya msonkhano. Magazi ena otsalawo awathire pa tsinde pa guwa lansembe zopsereza limene lili pa khomo la tenti ya msonkhano. 19Kenaka achotse mafuta onse a ng’ombeyo ndi kuwatentha pa guwa, 20ndipo achite ndi ng’ombe yayimunayi monga anachitira ndi ng’ombe yayimuna yopepesera machimo. Poto, wansembe adzapereka nsembe yopepesera anthu, ndipo machimo awo adzakhululukidwa. 21Kenaka atulutse ng’ombeyo kunjwa kwa msasa ndi kuyitentha monga anatenthera ng’ombe yoyamba ija. Imeneyi ndiyo nsembe yopepesera machimo a gulu lonse.

22“ ‘Ngati mtsogoleri achimwa mosadziwa nachita zimene ndi zoletsedwa ndi Yehova Mulungu wake, ndiye kuti wapalamula. 23Ndipo ngati wauzidwa za tchimo limene wachita, iye abwere ndi mbuzi yayimuna yopanda chilema kuti ikhale chopereka chake. 24Asanjike dzanja lake pa mutu wa mbuziyo ndi kuyiphera pamalo pamene amaphera zopereka zopsereza pamaso pa Yehova. Ichi ndi chopereka chopepesera tchimo. 25Pambuyo pake wansembe atengeko magazi a chopereka chopepesera tchimocho ndi chala chake, ndipo awapake pa nyanga za guwa lansembe zopsereza. Athire magazi otsalawo pa tsinde la guwalo. 26Wansembeyo atenthe mafuta onse pa guwapo monga amatenthera chopereka chachiyanjano. Pochita zimenezi, wansembe adzapereka nsembe yopepesera tchimo la munthuyo, ndipo adzakhululukidwa.

27“ ‘Ngati munthu wamba achimwa mosadziwa nachita zimene ndi zoletsedwa ndi Yehova, ndiye kuti wapalamula. 28Ndipo ngati wauzidwa za tchimo limene wachita, abweretse mbuzi yayikazi yopanda chilema kuti ikhale chopereka chopepesera tchimo. 29Asanjike dzanja lake pamutu pa mbuziyo ndipo ayiphe pamalo pamene amaphera chopereka chopsereza. 30Ndipo wansembe atenge magazazi ndi chala chake ndi kuwapaka pa nyanga za guwa lansembe zopsereza ndi kuthira magazazi wotsalawo pa tsinde la guwalo. 31Kenaka iye achotse mafuta onse monga momwe anachotsera mafuta a chopereka chachiyanjano, ndipo awatenthe pa guwa kuti akhale fungo lokomera Yehova. Potero, wansembe adzapereka nsembe yopepesera tchimo la munthuyo ndipo adzakhululukidwa.

32“ ‘Ngati munthu apereka mwana wankhosa ngati chopereka chopepesera tchimo lake, abwere ndi mwana wankhosa wamkazi wopanda chilema. 33Asanjike dzanja lake pa mutu wa mwana wankhosayo ndipo amuphe pamalo pamene amaphera chopereka chopsereza. 34Kenaka wansembe atengeko ndi chala chake magazazi a mwana wankhosa uja ndi kuwapaka pa nyanga za guwa lansembe zopsereza. Magazazi otsalawo athire pa tsinde la guwalo. 35Iye achotse mafuta onse, monga amachotsera mafuta a mwana wankhosa wa chopereka chachiyanjano, ndipo wansembe awatenthe pa guwa pamodzi ndi zopereka zina zopsereza za Yehova. Potero, wansembe adzapereka nsembe yopepesera tchimo limene munthuyo anachita ndipo adzakhululukidwa.

Phunziro 10

KUPEMBEZA: Kutamanda Yehova m'busa wathu

Masalimo 23: 1-6

Salimo 23

Salimo la Davide.

1 Yehova ndiye m'busa wanga, sindidzasowa kanthu.

2 Amandigoneka pa msipu wobiriwira,
amanditsogolera ku madzi akumwa abwino,

3 amatsitsimutsa moyo wanga.

Amanditsogolera m'njira zachilungamo
chifukwa cha dzina lake.

4 Ngakhale ndiyende

m'chigwa cha mdima wakuda bii,

sindidzaopa choyipa,

pakuti Inu muli ndi ine;

chibonga chanu ndi ndodo yanu

zimanditonthoza.

5 Mumandikonzera chakudya

adani anga akuona.

Mumadzoza mutu wanga ndi mafuta;

chikho changa chimasefukira.

6 Zoonadi, zokoma ndi chikondi chosasinthika zidzanditsata

masiku onse a moyo wanga,

ndipo ndidzakhala m'Nyumba ya Yehova

kwamuyaya.

Phunziro 11

CHIWOBOLO: Masomphenya a chisautso ndi ulemelero wa mtumiki wa Yehova

Yeseya 53

1Ndani wakhulupirira zimene tanenazi;
kapena ndani amene Yehova wamuzindikiritsa mphamvu zake?

2Iye anakula ngati mphukira pamaso pake,
ndiponso ngati muzu m'nthaka yowuma.

Iye analibe thupi labwino kapena nkhope yokongola yoti ife n'kumamuchewukira,
analibe maonekedwe woti ife n'kumamukhumbira.

3Iye ananyozedwa ndi kukanidwa ndi anthu,
munthu amene moyo wake unali wamasautso, wozolowera zowawa,
ndipo anali ngati munthu amene anzake amaphimba nkhope zawo akamuona.
Iye ananyozedwa, ndipo ife sitinamuyese kanthu.

4Ndithudi, iye anamva zowawa m'malo mwa ife;
ndipo anasautsidwa m'malo mwathu.

Koma ife tinkaganiza kuti ndi Mulungu amene akumulanga,
kumukantha ndi kumusautsa.

5Koma iye analasidwa chifukwa cha zolakwa zathu,
ndipo anamuzunza chifukwa cha zoyipa zathu;

iye analangidwa kuti ife tikhale ndi mtendere,
ndipo ndi mabala ake ife tinachiritsidwa.

6Ife tonse, ngati nkhoza, tasochera,
aliyense mwa ife akungodziyendera;
ndipo Yehova wamusenzetsa
zoyipa zathu zonse.

7Anthu anamuzunza ndi kumusautsa,
koma sanayankhule kanthu.

Monga mwana wankhosa wopita naye kokamupha amachitira,
kapena monga nkhoza imakhalira duu poyimeta,
momwemonso iye sanatsekule pakamwa pake.

8Atatha kumugwira mwankhanza ndikumuyimba mlandu, kenaka anapita naye
kukamupha.

Ndipo ndani amene analabadirako za zidzukululu zake,
poona kuti iye anachotsedwa m'dziko la anthu amoyo?

Ndani anaganizirapo poona kuti iye anakanthidwa chifukwa cha zolakwa za anthu anga?

9Anamukonzera manda ake pamodzi ndi anthu oyipa
ndipo anamuyika m'manda pamodzi ndi anthu achuma,
ngakhale kuti iye sanachite za chiwawa,
kapena kuyankhula za chinyengo.

10Komatu ndi Yehova amene anafuna kuti amuzunze ndi kumusautsa.

Yehova anapereka moyo wa mtumiki wake kuti ukhale nsembe yoperekedwa chifukwa
cha zolakwa.

Tsono iye adzaona zidzukululu zake ndipo adzakhala ndi moyo wautali,
ndipo chifuniro cha Yehova chidzachitika mwa iye.

11Atatha mazunzo a moyo wake,
adzaona kuwala, ndipo adzakhutira.

Mwa nzeru zake mtumiki wanga wolungamayo adzalungamitsa anthu ambiri,
popeza adzasenza zolakwa zawo.

¹²Motero Ine ndidzamupatsa ulemu pamodzi ndi akuluakulu,
adzagawana zofunkha ndi ankhondo amphamvu,
popeza anapereka moyo wake mpaka kufa,
ndipo anamuyika m'gulu la anthu olakwa kuti akhululukidwe.

Pakuti iye anasenza machimo a anthu ambiri,
ndipo anawapempherera anthu olakwa.

Phunziro 12

CHIWOMBOLO: Kubadwa kwa Yesu khristu

Luka 1:26-38, 2:1-20

Aneneratu za Kubadwa kwa Yesu

²⁶Mwezi wachisanu ndi chimodzi, Mulungu anatuma mngelo Gabrieli ku Nazareti, mudzi wa ku Galileya, ²⁷kwa namwali wopalidwa ubwenzi ndi Yosefe, wa fuko la Davide. Dzina la namwaliyo linali Mariya. ²⁸Mngeloyo anafika kwa iye nati, “Moni, inu amene Ambuye wakukomerani mtima kwambiri! Ambuye ali ndi inu.”

²⁹Mariya anavutika kwambiri ndi mawu awa ndipo anadabwa ndi kulonjera kotere. ³⁰Koma mngeloyo anati kwa iye, “Usachite mantha Mariya, pakuti wapeza chisomo pamaso Mulungu. ³¹Udzakhala woyembekezera ndipo udzabala mwana wamwamuna ndipo udzamupatse dzina loti Yesu. ³²Iye adzakhala wamkulu ndipo adzatchedwa Mwana wa Wammwambamwamba. Ambuye Mulungu adzamupatsa Iye mpando waufumu wa abambo ake Davide, ³³ndipo adzalamulira pa nyumba ya Yakobo ku nthawi zonse; ufumu wake sudzatha.”

³⁴Mariya anafunsa mngeloyo kuti, “Izi zingatheke bwanji popeza ine sindidziwa mwamuna?”

³⁵Mngelo anayankha kuti, “Mzimu Woyera adzabwera pa iwe ndipo mphamvu ya Wammwambamwamba idzakuphimba, ndipo Woyerayo amene adzabadwe adzatchedwa Mwana wa Mulungu. ³⁶Ngakhale Elizabeti m’bale wako adzakhala ndi mwana mu ukalamba wake ndipo iye amene amati ndi wosabereka, uno mwezi wake wachisanu ndi chimodzi. ³⁷Pakuti palibe chinthu chosatheka ndi Mulungu.”

³⁸Mariya anayankha kuti, “Ine ndine mtumiki wa Ambuye. Zikhale kwa ine monga mwanenera.”

Kubadwa kwa Yesu

¹M’masiku amenewo Kaisara Augusto anapereka lamulo kuti kalemba achitike m’dziko lonse la Aroma. ²(Uyu ndi kalemba woyamba amene anachitika pamene Kurenio anali bwanamkubwa wa Siriya). ³Ndipo aliyense anapita ku mzinda wa kwawo kukalembetsa.

⁴Choncho Yosefe anachoka ku Nazareti ku Galileya kupita ku Yudeya, ku Betelehemu ku mudzi wa Davide, chifukwa anali wa banja ndi fuko la Davide. ⁵Iye anapita kumeneko kukalembetsa pamodzi ndi Mariya, amene anapalana naye ubwenzi kuti akwatirane ndipo anali woyembekezera. ⁶Ali kumeneko, nthawi inakwana yakuti mwana abadwe, ⁷ndipo anabereka mwana wake woyamba, wamwamuna. Iye anamukulunga m’nsalu ndi kumuyika modyera ng’ombe, chifukwa kunalibe malo m’nyumba ya alendo.

Abusa ndi Angelo

⁸Ndipo kunali abusa amene amakhala ku dera lomwelo, kuyang’anira ziweto zawo usiku. ⁹Mngelo wa Ambuye anaonekera kwa iwo ndipo ulemerero wa Ambuye unawala mowazungulira. Iwo anachita mantha. ¹⁰Koma mngeloyo anawawuza kuti, “Musachite mantha. Ine ndakubweretserani Uthenga Wabwino wachimwemwe chachikulu umene udzakhala wa anthu onse. ¹¹Lero m’udzi wa Davide wakubwadwirani Mpulumutsi; Iye ndi Khristu Ambuye. ¹²Ichi chidzakhala chizindikiro kwa inu: mukapeza mwana wakhanda wokutidwa ndi nsalu atagona modyera ng’ombe.”

¹³Mwadzidzidzi gulu lalikulu la angelo linaonekera pamodzi ndi mngeloyo, kuyamika Mulungu ndi kumati,

¹⁴“Ulemerero kwa Mulungu mmwambamwamba,
ndi mtendere kwa anthu pa dziko lapansi amene Iye akondwera nawo.”

¹⁵Angelowo atabwerera kumwamba, abusawo anati kwa wina ndi mnzake, “Tiyeni ku Betelehemu tikaone zinthu zomwe zachitika, zimene Ambuye atiwuza ife.”

¹⁶Ndipo iwo anafulumira nyamuka nakapeza Mariya ndi Yosefe ndi mwana wakhanda, amene anagona modyera ng’ombe. ¹⁷Pamene anamuona Iye, iwo anafotokoza zomwe

anawuzidwa za mwanayo, ¹⁸ndipo onse amene anamva zimene abusawa ananena anadabwa. ¹⁹Koma Mariya anasunga zonsezi mu mtima mwake ndi kumazilingalira. ²⁰Abusa anabwerera, akulemekeza ndi kuyamika Mulungu chifukwa cha zonse anazimva ndi kuziona, zomwe zinali monga anawuzidwira ndi angelo aja.

Phunziro 13

CHIWOBOLO: Ubatizo wa Yesu khristu

Mateyu 3; Yohane 1:29-34

Yohane M'batizi

¹M'masiku amenewo, Yohane M'batizi anadza nalalikira m'chipululu cha Yudeya ²kuti, “Tembenukani mtima chifukwa ufumu wakumwamba wayandikira.” ³Uyu ndi amene mneneri Yesaya ananena za iye kuti,

“Mawu a wofuwula m'chipululu,
'Konzani njira ya Ambuye,
wongolani njira zake.’”

⁴Zovala za Yohane zinali zopangidwa ndi ubweya wa ngamira, ndipo amamangira lamba wachikopa m'chiwuno mwake. Chakudya chake chinali dzombe ndi uchi wa kuthengo. ⁵Anthu ankapita kwa iye kuchokera ku Yerusalemu ndi ku Yudeya konse ndi ku madera onse a Yorodani. ⁶Ndipo akavomereza machimo awo ankabatizidwa mu mtsinje wa Yorodani.

⁷Koma iye ataona Afarisi ndi Asaduki ambiri akubwera kumene ankabatiza, anawawuza kuti, “Ana a njoka inu! Ndani anakuchenjezani kuthawa mkwiyo umene ukubwera? ⁸Onetsani chipatso cha kutembenuka mtima. ⁹Ndipo musaganize ndi kunena mwa inu nokha kuti, ‘Tili nawo abambo athu Abrahamu.’ Ndina kwa inu kuti Mulungu akhoza kusandutsa miyala iyi kukhala ana a Abrahamu. ¹⁰Tikukamba pano nkhwangwa yayikidwa kale pa mizu ya mitengo, ndipo mtengo umene subala chipatso chabwino udulidwa ndi kuponyedwa pa moto.

¹¹“Ine ndikubatzani ndi madzi kusonyeza kutembenuka mtima. Koma pambuyo panga akubwera wina amene ali ndi mphamvu kuposa ine, amene sindiyenera kunyamula nsapato zake. Iyeyu adzakubatzani ndi Mzimu Woyera ndi moto. ¹²M'dzanja lake muli chopetera ndipo adzayeretsa popunthirapo pake nadzathira tirigu wake m'nkhokwe ndi kutentha zotsalira zonse ndi moto wosazima.”

Kubatizidwa kwa Yesu

¹³Pamenepo Yesu anabwera kuchokera ku Galileya kudzabatizidwa ndi Yohane mu mtsinje wa Yorodani. ¹⁴Koma Yohane anayesetsa kumukanira nati, “Ndiyenera kubatizidwa ndi Inu, bwanji Inu mubwera kwa ine?”

¹⁵Yesu anayankha kuti, **“Zibatero tsopano, ndi koyenera kwa ife kuchita zimenezi kukwaniritsa chilungamo chonse.”** Ndipo Yohane anavomera.

¹⁶Yesu atangobatizidwa, nthawi yomweyo potuluka m'madzi, kumwamba kunatsekuka ndipo taonani, Mzimu wa Mulungu anatsika ngati nkhunda natera pa lye. ¹⁷Ndipo mawu anamveka kuchokera kumwamba kuti, “Uyu ndiye mwana wanga wokondedwa amene ndikondwera naye.”

Yesu Mwana Wankhosa wa Mulungu

²⁹Pa tsiku lotsatira Yohane anaona Yesu akubwera kwa iye ndipo anati, “Taonani, Mwana Wankhosa wa Mulungu, amene achotsa tchimo la dziko lapansi! ³⁰Uyu ndi amene ndimatanthauza pamene ndinanena kuti, ‘Munthu amene akubwera pambuyo panga ndi wondiposa ine chifukwa analipo ine ndisanabadwe.’ ³¹Ine mwini sindinamudziwe lye, koma ndinabwera kubatiza ndi madzi kuti lye adziwike mu Israeli.”

³²Kenaka Yohane anapereka umboni uwu: “Ine ndinaona Mzimu Woyera ngati nkhunda kuchokera kumwamba nakhala pa lye. ³³Ine sindikanamudziwa lye, koma kuti amene anandituma ine kudzabatiza ndi madzi anati kwa ine, ‘Munthu amene udzaona Mzimu Woyera akutsika nakhazikika pa lye ndi amene adzabatize ndi Mzimu Woyera.’ ³⁴Ine ndaona ndipo ndikuchitira umboni kuti uyu ndi Mwana wa Mulungu.”

Phunziro 14

CHIWOBOLO: Kuyesedwa kwa Yesu khristu

Mateyu 4:1-11

Yesu Ayasedwa M'chipululu

¹Pambuyo pake Yesu anatsogozedwa ndi Mzimu Woyera kupita ku chipululu kukayesedwa ndi mdierekezi. ²Ndipo atasala kudya masiku makumi anayi usana ndi usiku, anamva njala. ³Woyesayo anadza kwa Iye nati, “Ngati ndinu mwana wa Mulungu, sandutsani miyala iyi kuti ikhale buledi.”

⁴Yesu anayankha kuti, “Zalembedwa, ‘Munthu sadzakhala ndi moyo ndi chakudya chokha, koma ndi mawu aliwonse ochokera m’kamwa mwa Mulungu.’ ”

⁵Pamenepo mdierekezi anapita naye ku mzinda woyera namuyimiritsa pamwamba penipeni pa Nyumba ya Mulungu. ⁶Ndipo anati, “Ngati ndinu Mwana wa Mulungu, dziponyeni nokha pansu. Pakuti kwalembedwa:

“ ‘Adzalamulira angelo ake za iwe,
ndipo adzakunyamula ndi manja awo
kuti phazi lako lisagunde pa mwala.’ ”

⁷Yesu anamuyankha kuti, “Kwalembedwanso: ‘Musamuyese Yehova Mulungu wanu.’ ”

⁸Kenaka mdierekezi anamutengera Yesu ku phiri lalitali kwambiri namuonetsa maufumu onse a dziko lapansi ndi ulemero wawo. ⁹Ndipo anati kwa Iye, “Zonsezi ndidzakupatsani ngati mutandiweramira ndi kundipembedza ine.”

¹⁰Yesu anati kwa Iye, “Choka Satana! Zalembedwa, ‘Pembedza Yehova Mulungu wako ndi kumutumikira Iye yekha.’ ”

¹¹Pamenepo mdierekezi anamusiya ndipo angelo anamutumikira Iye.

Phunziro 15

CHIWOBOLO: Yesu ayimitsa namondwe

Maliko 4:35-41

Yesu Aletsa Namondwe

³⁵Tsiku limenelo atafika madzulo, anawuza ophunzira ake kuti, “**Tiyeni tiwolokere tsidya lina.**” ³⁶Atasiya gulu la anthu m’mbuyo, anamutenga lye, napita naye monga momwe anali m’bwatolo. Panalinso mabwato ena pamodzi ndi lye. ³⁷Mphepo yamkuntho inabuka, ndipo mafunde anawomba bwatolo, kotero kuti linali pafupi kumira. ³⁸Pa nthawi imeneyi Yesu anali akugona atatsamira pilo kumbuyo kwa bwato. Ophunzira anamudzutsa nati kwa lye, “Aphunzitsi, kodi simukusamala kuti timira?”

³⁹Yesu anauka nadzudzula mphepo nati kwa mafunde, “**Chete! Khala bata!**” Pamenepo mphepo inaleka ndipo kunachita bata.

⁴⁰lye anati kwa ophunzira ake, “**Muli ndi mantha chifukwa chiyani? Kodi mukanalibe chikhulupiriro?**”

⁴¹Iwo anachita mantha nafunsana wina ndi mnzake kuti, “Uyu ndani? Ngakhale mphepo ndi nyanja zimumvera lye!”

Phunziro 16

CHIWOBOLO: Yesu atulutsa ziwanda

Maliko 5:1-20

Yesu Achiritsa Wogwidwa ndi Ziwanda

¹Ndipo anawoloka nyanja napita ku dera la Gerasa. ²Yesu atatuluka m'bwato, munthu amene anali ndi mzimu woyipa anachoka ku manda ndi kukumana naye. ³Munthuyu amakhala ku manda, ndipo panalibe amene akanatha kumumanganso ngakhale ndi unyolo. ⁴Pakuti nthawi zambiri akamumanga manja ndi miyendo amadula maunyolo ndi kudula zitsulo zimene zinali m'mapazi ake. Panalibe amene anali ndi mphamvu yoti ndi kumugonjetsa. ⁵Usana ndi usiku ankakhala ku manda ndi kumapiri, akulira ndi kudzicheka ndi miyala.

⁶Ataona Yesu ali patali, anathamanga nagwa pa mawondo ake pamaso pake. ⁷Iye anafuwula kwambiri nati, "Mukufuna muchite nane chiyani, Yesu Mwana wa Mulungu Wammwambamwamba? Lumbirani kwa Mulungu kuti simundizunza!" ⁸Pakuti Yesu anati kwa iye, "Tuluka mwa munthuyu, iwe mzimu woyipa!"

⁹Ndipo Yesu anamufunsa iye, "Dzina lako ndani?"

Iye anayankha kuti, "Dzina langa ndine Legiyo, pakuti tilipo ambiri." ¹⁰Ndipo anamupempha Yesu mobwerezabwereza kuti asazitulutse m'deralo.

¹¹Gulu lalikululu la nkumba limadya m'mbali mwa phiri limene linali pafupi. ¹²Ziwandazo zinapempha Yesu kuti, "Titumizeni pakati pa nkumbazo; ndipo mutilole tilowe mwa izo." ¹³Iye anazipatsa chilolezo, ndipo mizimu yoyipayo inatuluka ndi kukalowa mu nkumbazo. Gulu la nkumba, zokwana pafupifupi 2,000 zinathamanga kutsetserekerera ku nyanja ndipo zinamira.

¹⁴Omwe amaweta nkumbazo anathawa ndi kukawuza anthu za izi mu mzinda ndi ku madera a ku midzi, ndipo anthu anapita kukaona zomwe zinachitika. ¹⁵Atafika kwa Yesu, anaona munthu amene anagwidwa ndi ziwanda zambiri uja atakhala pansu pomwepo, atavala, ndipo ali bwinobwino. Iwo anachita mantha. ¹⁶Amene anaona zimenezi anawuza anthu zomwe zinachitika kwa munthu wogwidwa ndi ziwandayo ndipo anawawuzanso za nkumbazo. ¹⁷Ndipo anthu anayamba kumupempha Yesu kuti achoke m'dera lawo.

¹⁸Yesu akulowa m'bwato, munthu amene anagwidwa ndi ziwanda uja anamupempha kuti apite nawo. ¹⁹Yesu sanamulole, koma anati, "Pita kwanu ku banja lako ndipo ukawawuze zimene Ambuye wakuchitira, ndi chifundo chimene wakuchitira." ²⁰Pomwepo munthuyo anapita nayamba kuwuzana anthu a ku Dekapoli zinthu zimene Yesu anamuchitira. Ndipo anthu onse anadabwa.

Phunziro 17

CHIWOBOLO: Yesu achulukitsa mikate

Yohane 6:1-37

Yesu Adyetsa Anthu 5,000

¹Nthawi ina zitatha izi, Yesu anawolokera ku gombe la kutali la nyanja ya Galileya (iyi ndi nyanja ya Tiberiya), ²ndipo gulu lalikulu la anthu linamutsata lye chifukwa linaona zizindikiro zodabwitsa zimene anazichita pa odwala. ³Kenaka Yesu anakwera pa phiri nakhala pansu ndi ophunzira ake. ⁴Tsopano phwando la Paska la Ayuda linali pafupi.

⁵Yesu atakweza maso ndi kuona gulu lalikulu la anthu likubwera kwa lye, anati kwa Filipino, **“Kodi tingagule kuti buledi kuti anthu awa adye?”** ⁶Iye anafunsa izi kumuyesa chabe, pakuti lye ankadziwa chimene ankayenera kuchita.

⁷Filipo anamuyankha lye kuti, **“Malipiro a miyezi isanu ndi itatu sangathe kugula buledi okwanira aliyense kuti adye!”**

⁸Mmodzi wa ophunzira ake, Andreyo, m’bale wa Simoni Petro, anati, ⁹“Pano pali mnyamata amene ali ndi buledi musanu wabarele ndi tinsomba tiwiri, kodi zingakwane onsewa?”

¹⁰Yesu anati, **“Awuzeni anthuwa akhale pansu.”** Pamalo pamenepa panali udzu wambiri ndipo amuna amene anakhala pansu anali osachepera 5,000. ¹¹Kenaka Yesu anatenga bulediyo, atayamika anagawira iwo amene anakhala pansu, chimodzimodzinso nsombazo monga momwe iwo anafunira.

¹²Ndipo atakhuta, lye anati kwa ophunzira ake, **“Tolani zotsala kuti pasawonongeke kanthu.”** ¹³Choncho iwo anasonkhanitsa makombo nadzaza madengu khumi ndi awiri.

¹⁴Pambuyo pake anthu ataona chizindikiro chodabwitsa chimene Yesu anachita, iwo anati, **“Zoonadi uyu ndi Mneneri wakudzayo m’dziko la pansu.”** ¹⁵Yesu atadziwa kuti iwo amafuna kubwera kudzamuwumiriza kuti akhale mfumu, anachoka napita ku phiri pa yekha.

Yesu Ayenda pa Madzi

¹⁶Pofika madzulo, ophunzira ake anatsikira ku nyanja, ¹⁷kumene iwo analowa m’bwato ndi kuyamba kuwoloka nyanja kupita ku Kaperenawo. Tsopano kunali kutada ndipo Yesu anali asanabwerere kwa iwo. ¹⁸Mphepo yamphamvu inawomba ndipo nyanja inalusa. ¹⁹Iwo atayenda makilomita asanu kapena asanu ndi limodzi, anaona Yesu akuyandikira bwatolo, akuyenda pa madzi; ndipo anachita mantha. ²⁰Koma lye anawawuza kuti, **“Ndine, musaope.”** ²¹Ndipo iwo analola kumutenga m’bwatomo, nthawi yomweyo bwatolo linafika ku gombe la nyanja kumene ankapita.

²²Pa tsiku lotsatira gulu la anthu limene linatsala kumbali ina yanyanjayo linaona kuti panali bwato limodzi lokha, ndipo kuti Yesu sanalowe m’bwatomo pamodzi ndi ophunzira ake, koma kuti ophunzirawo anapita okha. ²³Kenaka mabwato ena ochokera ku Tiberiya anafika pafupi ndi pamalo pamene anthu anadya buledi Ambuye atayamika. ²⁴Nthawi yomwe gulu la anthu linaona kuti Yesu kapena ophunzira ake sanali pamenepo, ilo linalowanso m’mabwatowo ndi kupita ku Kaperenawo kukamufunafuna Yesu.

Yesu Chakudya Chamoyo

²⁵Atamupeza mbali ina ya yanyanjayo, iwo anamufunsa lye kuti, **“Rabi, mwafika nthawi yanji kuno?”**

²⁶Yesu anawayankha kuti, **“Zoonadi, Ine ndikukuwuzani kuti mukundifuna, osati chifukwa munaona zizindikiro zodabwitsa koma chifukwa munadya chakudya ndi kukhuta.** ²⁷Gwirani ntchito, osati chifukwa cha chakudya chimene chimawonongeka koma chifukwa cha chakudya chimene sichiwonongeka mpaka ku moyo wosatha, chimene Mwana wa Munthu adzakupatsani. **Mulungu Atate anamusindikiza chizindikiro chomuvomereza.”**

²⁸Kenaka anamufunsa lye kuti, **“Kodi tichite chiyani kuti tigwire ntchito za Mulungu?”**

²⁹Yesu anayankha kuti, **“Ntchito ya Mulungu ndi iyi: Kukhulupirira lye amene anamutuma.”**

³⁰Choncho iwo anamufunsa lye kuti, “Kodi mudzatipatsa chizindikiro chodabwitsa chotani kuti ife tichione ndi kukhulupirira Inu? Kodi mudzachita chiyani? ³¹Makolo athu akale anadya mana m’chipululu; monga zalembedwa: ‘anawapatsa buledi wochokera kumwamba kuti adye.’”

³²Yesu anawawuza kuti, “Zoonadi, Ine ndikukuwuzani kuti si Mose amene ankakupatsani chakudya chochokera kumwamba, koma ndi Atate anga amene ankakupatsani chakudya chenicheni chochokera kumwamba. ³³Pakuti chakudya cha Mulungu ndi lye amene wabwera kuchokera kumwamba ndi kupereka moyo ku dziko la pansu.”

³⁴Iwo anati, “Ambuye, kuyambira tsopano muzitipatsa buledi ameneyu.”

³⁵Kenaka Yesu ananenetsa kuti, “Ine ndine chakudya chamoyo. lye amene abwera kwa Ine sadzamva njala, ndipo iye amene akhulupirira Ine sadzamva ludzu. ³⁶Monga ndakuwuzani kale, ngakhale kuti mwandiona simukukhulupirabe. ³⁷Zonse zimene Atate andipatsa zidzabwera kwa Ine, ndipo aliyense amene adzabwera kwa Ine sindidzamutaya kunja.

Phunziro 18

CHIWOBOLO: Yesu achiritisa odwala ndikukhulukira machimo

Luka 5:17-26

Yesu Achiritisa Wofa Ziwalo

¹⁷Tsiku lina pamene ankaphunzitsa, Afarisi ndi aphunzitsi amalamulo, amene anachokera ku midzi yonse ya Galileya ndi ku Yudeya ndi Yerusalemu, anakhala panso pomwepo. Ndipo mphamvu ya Ambuye inalipo yakuti Iye achiritse odwala. ¹⁸Amuna ena anabwera atanyamula munthu wofa ziwalo pa mphasa ndipo anayesa kumulowetsa m'nyumba kuti amugoneke pamaso pa Yesu. ¹⁹Atalephera kupeza njira yochitira zimenezi chifukwa cha gulu la anthu, anakwera naye pa denga ali pa mphasa pomwepo ndi kumutsitsira m'kati pakati pa gulu la anthu, patsogolo penipeni pa Yesu.

²⁰Yesu ataona chikhulupiriro chawo, anati, **“Mnzanga, machimo ako akhulukidwa.”**

²¹Afarisi ndi aphunzitsi amalamulo anayamba kuganiza mwa iwo okha kuti, “Kodi munthu uyu ndi ndani amene ayankhula zamwano? Kodi ndani amene angakhulukire machimo kupatula Mulungu?”

²²Yesu anadziwa zomwe iwo amaganiza ndipo anafunsa kuti, **“Kodi ndi chifukwa chiyani mukuganiza zimenezi m'mitima mwanu? ²³Kodi chapafupi ndi chiti: kunena kuti, ‘Machimo ako akhulukidwa,’ kapena kunena kuti, ‘Nyamuka ndipo yenda?’”** ²⁴Koma kuti inu mudziwe kuti **Mwana wa Munthu ali ndi ulamuliro pa dziko lapansi wokhulukira machimo, Iye anati kwa munthu wofa ziwalo, “Ine ndikuwuzwa iwe kuti, ‘Imirira, nyamula mphasa ndipo uzipita kwanu.’”** ²⁵Nthawi yomweyo anayimirira patsogolo pawo, nanyamula mphasa yake ndipo anapita kwawo akuyamika Mulungu. ²⁶Aliyense anadabwa ndi kuchita mantha ndipo anayamika Mulungu. Iwo anadabwa kwambiri ndipo anati, “Lero taona zinthu zosayiwalika.”

Phunziro 19

CHIWOBOLO: Yesu ndi asamaliya

Yohane 4:1-26, 39-42

Yesu Acheza ndi Mayi wa ku Samariya

¹Yesu atazindikira kuti Afarisi amva zoti Iye ankapeza ndi kubatiza ophunzira ambiri kupambana Yohane, ²(ngakhale kuti Yesuyo sankabatiza, koma ophunzira ake). ³Iye anachoka ku Yudeya ndi kubwereranso ku Galileya.

⁴Ndipo Iye anayenera kudutsa mu Samariya. ⁵Iye anafika m'mudzi wa Asamariya wotchedwa Sukari, pafupi ndi malo amene Yakobo anapatsa mwana wake Yosefe. ⁶Chitsime cha Yakobo chinali pamenepo ndipo Yesu atatopa ndi ulendo anakhala panso pambali pa chitsimecho. Nthawi inali pafupifupi ora lachisanu ndi chimodzi masana.

⁷Mayi wa Chisamariya atabwera kudzatunga madzi, Yesu anati kwa iye, **"Kodi ungandipatse madzi akumwa."** ⁸(Ophunzira ake n'kuti atapita m'mudzi kukagula chakudya).

⁹Mayiyo anati kwa Iye, "Inu ndinu Myuda ndipo ine ndine Msamariya. Bwanji mukundipempha madzi akumwa?" (Popeza Ayuda ndi Asamariya sankayanjana).

¹⁰Yesu anamuyankha kuti, **"Koma iwe ukanadziwa mphatso ya Mulungu ndi Iye amene akukupempha madzi akumwa, ukanamupempha ndipo akanakupatsa madzi amoyo."**

¹¹Mayiyo anati, "Ambuye, Inu mulibe kanthu kotungira madzi ndipo chitsime ndi chakuya. Kodi madzi amoyowo mungawatenge kuti? ¹²Kodi Inu ndinu wamkulu kuposa kholo lathu Yakobo, amene anatipatsa chitsimechi ndipo iye ankamwanso monga anachita ana ake ndi ziweto zake?"

¹³Yesu anayankha kuti, **"Aliyense amene amamwa madzi awa amamvanso ludzu, ¹⁴koma aliyense amene adzamwa madzi amene Ine ndidzamupatsa sadzamvanso ludzu. Ndithudi, madzi amene ndidzamupatsa adzakhala kasupe wamadzi wotumphukira ku moyo wosatha."**

¹⁵Mayiyo anati kwa Iye, "Ambuye, patseni madzi amenewo kuti ndisadzamvenso ludzu ndi kumabwerabe kuno kudzatunga madzi."

¹⁶Iye anamuwuzwa kuti, **"Pita kayitane mwamuna wako ndipo ubwere naye."**

¹⁷Iye anayankha kuti, "Ine ndiliba mwamuna."

Yesu anati kwa iye, **"Wakhoza ponena kuti ulibe mwamuna. ¹⁸Zoona n'zakuti iwe wakhala pa banja ndi amuna asanu, ndipo mwamuna amene uli naye tsopano si wako. Zimene wanenazi ndi zoona."**

¹⁹Mayiyo anati, "Ambuye, ine ndazindikira kuti Inu ndinu mneneri. ²⁰Makolo athu ankapembedza m'phiri ili koma inu Ayuda mumati malo amene tiyenera kupembedzera ali ku Yerusalemu."

²¹Yesu anati, **"Mayi inu khulupirira Ine. Nthawi ikubwera pamene inu simudzapembedza Atate m'phiri ili kapena mu Yerusalemu. ²²Inu Asamariya mumapembedza chimene simukuchidziwa. Ife timapembedza chimene tikuchidziwa, pakuti chipulumutso n'chochokera kwa Ayuda. ²³Koma nthawi ikubwera ndipo yafika kale tsopano pamene opembedza woona adzapembedza Atate mu mzimu ndi m'choonadi, pakuti opembedza otere ndiwo amene Atate akuwafuna. ²⁴Mulungu ndi Mzimu, ndipo omupembedza Iye ayenera kumupembedza mu mzimu ndi m'choonadi."**

²⁵Mayiyo anati, "Ine ndikudziwa kuti Mesiya (wotchedwa Khristu) akubwera. Akabwera, Iye adzafotokoza zonse kwa ife."

²⁶Ndipo Yesu anamuwuzwa kuti, **"Amene ndikukuyankhulane, ndine amene."**

Asamariya Ambiri Akhulupirira

³⁹Asamariya ambiri ochokera m'mudziwo anakhulupirira Iye chifukwa cha umboni wa mayiyo wakuti, "Iye anandiwuzwa ine zonse ndinazichita." ⁴⁰Choncho Asamariya atabwera kwa Iye, anamuwumiriza Iye kuti akhale nawo, ndipo Iye anakhala nawo masiku awiri. ⁴¹Ndipo chifukwa cha mawu ake, ena ambiri anakhulupirira.

42Iwo anati kwa mayiyo, “Ife sitikukhulupirira chifukwa cha mawu ako okha, koma tsopano ife tadzimvera tokha, ndipo tikudziwa kuti munthu uyu ndithu ndi Mpulumutsi wa dziko lapansi.”

Phunziro 20

CHIWOBOLO: Yesu aphunzitsa za njira ya Mulungu

Luke 10:25-37; 15:11-32

Fanizo la Msamariya Wachifundo

²⁵Nthawi ina katswiri wa malamulo anayimirira kuti ayese Yesu. Iye anati, “Aphunzitsi, ndichite chiyani kuti ndikhale ndi moyo wosatha?”

²⁶Yesu anayankha kuti, “**Mwalembedwa chiyani m'Malamulo, ndipo iwe umawerenga zotani?**”

²⁷Iye anayankha kuti, “Uzikonda Yehova Mulungu wako ndi mtima wako wonse, ndi moyo wako wonse, ndi mphamvu zako zonse ndi nzeru zako zonse, ndi kukonda mnansi wako monga iwe mwini.”

²⁸Yesu anayankha kuti, “**Iwe wayankha bwino, chita zimenezi ndipo udzakhala ndi moyo.**”

²⁹Koma iye anafuna kudzilungamitsa yekha, ndipo anamufunsanso Yesu kuti, “Kodi mnansi wanga ndani?”

³⁰Yesu pomuyankha anati, “Munthu wina ankatsikira ku Yeriko kuchokera ku Yerusalemu. Pa njira anavulazidwa ndi achifwamba. Anamuvula zovala zake, namumenya ndi kuthawa, namusiya ali pafupi kufa. ³¹Wansembe ankapita pa njira yomweyo, ndipo ataona munthuyo, analambalala. ³²Chimodzimodzinso, Mlevi wina pamene anafika pa malopo ndi kumuona, analambalalanso. ³³Koma Msamariya wina, ali pa ulendo wake, anafika pamene panali munthuyo; ndipo atamuona, anamva naye chisoni. ³⁴Anapita panali munthu wovulalayo, nathira mafuta ndi vinyo pa zilonda zake, n'kuzimanga. Kenaka anamukweza pa bulu wake, napita naye ku nyumba ya alendo, namusamalira. ³⁵Mmawa mwake anatenga ndalama ziwiri zasiliva nazipereka kwa woyang'anira nyumbayo, nati, 'Musamalireni munthuyu, ndipo pobwera ndidzakubwezerani zonse zimene mugwiritse ntchito.'

³⁶“Kodi ukuganiza ndi ndani mwa atatuwa, amene anali mnansi wa munthu amene anavulazidwa ndi achifwambawo?”

³⁷Katswiri wa Malamulo uja anayankha kuti, “Amene anamuchitira chifundo.”

Yesu anamuwuzza kuti, “Pita, uzikachita chimodzimodzi.”

Fanizo la Mwana Wolowerera

¹¹Yesu anapitiriza kunena kuti, “Panali munthu amene anali ndi ana aamuna awiri. ¹²Wamng'onoyo anati kwa abambo ake, 'Abambo, patseni gawo langa la chuma chanu.' Ndipo iye anawagawira awiriwo chuma chawo.

¹³“Pasanapite nthawi, wamng'onoyo anasonkhanitsa chuma chake chonse, napita ku dziko lakutali ndipo kumeneko anayamba kumwaza chuma chake m'njira zachitayiko. ¹⁴Iye atawononga zonse, kunagwa njala yoopsa m'dziko lonselo ndipo anayamba kusauka. ¹⁵Iye anapita kwa nzika ina ya dzikolo nakakhala naye ndi kumagwira ntchito, amene anamutumiza ku munda kukadyetsa nkumba. ¹⁶Iye analakalaka atakhutitsa mimba yake ndi makoko amene nkumbazo zinkadya, koma panalibe wina amene anamupatsa kanthu.

¹⁷“Maganizo ake atabweramo, iye anati, 'Ndi antchito angati a abambo anga amene ali ndi chakudya chimene amadya n'kutsalako ndipo ine ndili pano kufa ndi njala! ¹⁸Ine ndinyamuka ndi kubwerera kwa abambo anga ndipo ndikati kwa iwo: abambo, ine ndachimwira kumwamba ndi kwa inu. ¹⁹Ndine wosayeneranso kutchedwa mwana wanu; munditenge ngati mmodzi wa antchito anu.' ²⁰Ndipo iye ananyamuka ndi kupita kwa abambo ake.

“Koma iye akanali patali, abambo ake anamuona ndipo anamvera chisoni; anathamangira mwanayo, namukumbatira ndi kupsompona.

²¹“Mwanayo anati, 'Abambo, ine ndachimwira kumwamba ndi inunso. Ine sindiyenera konse kutchedwa mwana wanu.'

²²“Koma abambowo anati kwa antchito ake, 'Fulumirani! Bweretsani mkanjo wabwino kwambiri ndipo mumuveke. Muvekeni mphete ndi nsapato. ²³Bweretsani mwana wang'ombe

wonenepa ndipo iphani. Tiyeni tikhale ndi phwando ndi kukondwerera. ²⁴Pakuti mwana wangayu anali wakufa, ndipo ali ndi moyonso; iye anatayika ndipo wapezeka.’ Chomwecho anayamba kukondwerera.

²⁵ “Nthawi imeneyi, mwana wake wamkulu uja anali ku munda. Iye atafika pafupi ndi nyumba, anamva anthu akuyimba ndi kuvina. ²⁶Ndipo iye anayitana mmodzi wa antchito, namufunsa chimene chimachitika. ²⁷Iye anayankha kuti, ‘M’bale wako wabwera ndipo abambo ako apha mwana wang’ombe wonenepa chifukwa wabwera wamoyo ndipo ali bwino.’

²⁸ “Mwana wamkulu anakwiya ndipo anakana kulowa. Chomwecho abambo ake anatuluka ndi kumudandaulira. ²⁹Koma iye anayankha abambo ake kuti, ‘Taonani! Zaka zonsezi ndakhala ndikukutumikirani kugwira ntchito yowawa ndipo palibe pamene sindinamvere malamulo anu. Koma inu simunandipatse ngakhale mwana wambuzi kuti ine ndichite phwando ndi anzanga. ³⁰Koma pamene mwana wanu uyu amene wawononga chuma chanu ndi achiwerewere wabwera ku nyumba, inu mwamuphera mwana wang’ombe wonenepa.’ ”

³¹ Abambowo anati, “Mwana wanga, iwe umakhala ndi ine nthawi zonse ndipo zonse ndili nazo ndi zako. ³²Koma tinayenera kukondwera ndi kusangalala, chifukwa m’bale wako uyu anali wakufa ndipo ali ndi moyonso; iye anali wotayika ndipo wapezeka.”

Phunziro 21

CHIWOBOLO: Yesu aphunzitsa kupemphera

Luka 18:9-14; Yohane 16:24

Fanizo la Mfarisi ndi Wolandira Msonkho

⁹Yesu ananena fanizoli kwa amene amadzikhulupirira mwa iwo okha kuti anali wolungama nanyoza ena onse. ¹⁰“Anthu awiri anapita ku Nyumba ya Mulungu kukapemphera, wina Mfarisi ndi winayo wolandira msonkho. ¹¹Mfarisiyo anayimirira ndipo anapemphera za iye mwini kuti, ‘Mulungu, ine ndikuyamika kuti sindili ngati anthu ena onse, achifwamba, ochita zoyipa, achigololo, sindilinso ngati wolandira msonkhoyu. ¹²Ine ndimasala kudya kawiri pa Sabata ndipo ndimapereka chakhumi pa zonse ndimapeza.’

¹³“Koma wolandira msonkhoyo ali chiyimire potero, sanathe n’komwe kuyang’ana kumwamba; koma anadziguguda pachifuwa ndipo anati, ‘Mulungu, chitireni chifundo, ine wochimwa.’

¹⁴“Ine ndikukuwuzani kuti munthu wolandira msonkhoyu, osati Mfarisiyu, anapita kwawo atalungamitsidwa pamaso pa Mulungu. Chifukwa chake, aliyense wodzikweza adzachedpetsedwa, ndipo wodzichepetsa adzakwezedwa.”

²⁴Mpaka tsopano simunapemphe kalikonse m’dzina langa. Pemphani ndipo mudzalandira, ndipo chimwemwe chanu chidzakhala chathunthu.

Phunziro 22

CHIWOBOLO: Yesu aphunzitsa zachifundo, kupemphera ndi kusala kudya

Mateyu 6:1-34

Zopereka Zachifundo

¹ “Samalani kuti musachite ntchito zanu zolungama pamaso pa anthu kuti akuoneni. Popeza ngati mutero simudzalandira mphotho yochokera kwa Atate anu akumwamba.

² “Pamene mupereka zachifundo, musachite modzionetsera monga amachita achiphamaso m’masunagoge ndi pa misewu kuti atamidwe ndi anthu. Zoonadi, Ine ndikuwuzani kuti iwowo alandiriratu mphotho yawo yonse. ³Koma pamene mupereka zachifundo, dzanja lanu lamanzere lisadziwe chimene dzanja lanu lamanja likuchita, ⁴kotero kuti kupereka kwanu kukhale mwachinsinsi. Ndipo Atate anu amene amaona zochitika mwachinsinsi, adzakupatsani mphotho.

Za Kupemphera

⁵ “Pamene mupemphera, musakhale ngati achiphamaso, chifukwa iwo amakonda kupemphera choyimirira m’masunagoge ndi pa mphambano za m’misewu kuti anthu awaone. Zoonadi, Ine ndikuwuzani kuti iwo alandiriratu mphotho yawo yonse. ⁶Koma pamene mupemphera, lowani m’chipinda chanu cham’kati, ndi kutseka chitseko ndipo mupemphere kwa Atate anu amene saoneka. Ndipo Atate anu, amene amaona zochitika mseri, adzakupatsani mphotho. ⁷Ndipo pamene mukupemphera, musamabwerezabwereza monga akunjya, pakuti iwo amaganiza kuti adzamveka chifukwa chochulutsa mawu. ⁸Musakhale ngati iwo chifukwa Atate anu amadziwa zimene musowa musanapemphe.

⁹ “Chifukwa chake pempherani motere:

“ ‘Atate athu akumwamba,
dzina lanu lilemekezedwe,

¹⁰ Ufumu wanu ubwere,
chifuniro chanu chichitike

pansi pano monga kumwamba.

¹¹ Mutipatse chakudya chatu chalero.

¹² Mutikhulukire mangawa athu,
monga ifenso tawakhulukira amangawa athu.

¹³ Ndipo musatitengere kokatiyesa;
koma mutipulumutse kwa woyipayo.’

¹⁴ Ngati inu mukhulukira anthu pamene akuchimwirani, Atate anu akumwamba adzakukhulukirani. ¹⁵Koma ngati inu simukhulukira anthu zolakwa zawo, Atate anunso sadzakukhulukirani machimo anu.

Kusala Kudya

¹⁶ “Pamene mukusala kudya, musaonetse nkhope yachisoni monga achita achiphamaso, pakuti iwo amasinthana nkhope zawo kuonetsa anthu kuti akusala kudya. Zoonadi, Ine ndikuwuzani kuti iwo alandiriratu mphotho yawo yonse. ¹⁷Koma pamene ukusala kudya, samba m’maso nudzole mafuta kumutu, ¹⁸kuti usaonekere kwa anthu kuti ukusala kudya koma kwa Atate ako ali mseri; ndipo Atate ako amene amaona za mseri adzakupatsa mphotho.

Za Chuma cha Kumwamba

¹⁹ “Musadziwunjikire chuma pa dziko lapansi, pamene njenjete ndi dzimbiri zimawononga ndi pamene mbala zimathyola ndi kuba. ²⁰Koma mudziwunjikire chuma kumwamba kumene njenjete ndi dzimbiri siziwononga ndipo mbala sizithyola ndi kuba. ²¹Pakuti kumene kuli chuma chako, mtima wako udzakhala komweko.

Diso Nyale ya Thupi

²² “Diso ndi nyale ya thupi. Ngati maso ako ali bwino, thupi lako lonse lidzakhala m’kuwala. ²³Koma ngati maso ako sali bwino, thupi lako lonse lidzakhala mu mdima. Koma ngati kuwala kuli mwa iwe ndi mdima, ndiye kuti mdimawo ndi waukulu bwanji!

²⁴ “Palibe munthu angathe kukhala kapolo wa ambuye awiri. Pakuti pena adzamuda mmodzi ndi kukonda winayo kapena adzagwira ntchito mokhulupirika kwa mmodzi, nadzanyoza winayo. Simungathe kukhala kapolo wa Mulungu ndi wa chuma pa nthawi imodzi.

Musade Nkhawa

²⁵ “N’chifukwa chake ndikuwuzani kuti musadere nkhawa za moyo wanu kuti mudzadya chiyani kapena mudzamwa chiyani; kapenanso za thupi lanu kuti mudzavala chiyani. Kodi moyo suposa chakudya? Kodi thupi siliposa zovala? ²⁶Onani mbalame zamlengalenga sizifesa kapena kukolola kapena kusunga m’nkhekwe komabe Atate anu akumwamba amazidyetsa. Kodi inu simuziposa kwambiri? ²⁷Kodi ndani wa inu podandaula angathe kuwonjeza ora limodzi pa moyo wake?

²⁸ “Ndipo bwanji inu mudera nkhawa za zovala? Onani makulidwe a maluwa akutchire. Sagwira ntchito kapena kuwomba nsalu. ²⁹Ndikukuwuzani kuti angakhale Solomoni mu ulemero wake sanavale mofanana ndi limodzi la maluwa amenewa. ³⁰Ngati umu ndi mmene Mulungu avekera udzu wa kutchire umene ulipo lero ndipo mawa uponyedwa ku moto, kodi sadzakuvekani koposa? Aa! Inu a chikhulupiriro chochepa! ³¹Chifukwa chake musadere nkhawa ndi kuti, ‘Tidzadya chiyani?’ kapena ‘Tidzamwa chiyani?’ kapena ‘Tidzavala chiyani?’ ³²Pakuti anthu akunja amazifuna zinthu zonsezi ndipo Atate anu akumwamba adziwa kuti musowa zimenezi. ³³Koma muyambe mwafuna ufumu wake ndi chilungamo chake ndipo zinthu zonsezi zidzapatsidwa kwa inu. ³⁴Chifukwa chake musadere nkhawa ndi za mawa, popeza tsiku lililonse lili ndi zovuta zake zokwanira.

Phunziro 23

CHIWOBOLO: Yesu aukitsa wakufa

Yohane 11:1-44

Imfa ndi Kuukitsidwa kwa Lazaro

¹Tsopano munthu wina dzina lake Lazaro anadwala. Iye anali wa ku Betaniya, mudzi wa Mariya ndi mchemwali wake Marita. ²Mariyayo ndi yemwe uja amene anadzoza Ambuye ndi mafuta onunkhira napukuta mapazi ake ndi tsitsi lake. Lazaro wodwalayo anali mlongo wake. ³Choncho alongo ake anatumiza mawu kwa Yesu kuti, “Ambuye, uja amene Inu mumamukonda akudwala.”

⁴Atamva izi, Yesu anati, **“Kudwalako safa nako. Koma akudwala kuti Mulungu alemekedwe; ndi kuti Mwana wa Mulungu alemekedwe chifukwa cha matendawo.”** ⁵Yesu anakonda Marita, mchemwali wake ndi Lazaro. ⁶Koma atamva kuti Lazaro akudwala, Iye anakhalabe kumene anali masiku ena awiri.

⁷Kenaka anati kwa ophunzira ake, **“Tiyeni tibwerere ku Yudeya.”**

⁸Ophunzira akewo anati, “Rabi, posachedwa pomwepa Ayuda anafuna kukugendani ndi miyala, koma Inu mukupitanso komweko?”

⁹Yesu anayankha kuti, **“Kodi sipali maora khumi ndi awiri pa tsiku? Munthu amene amayenda masana sapunthwa, popeza akuona chifukwa cha kuwala kwa dziko lapansi. ¹⁰Koma amene akuyenda usiku amapunthwa, chifukwa kuwalako alibe.”**

¹¹Iye atatha kunena izi, anapitirira kuwawuza iwo kuti, **“Bwenzi lathu Lazaro wagona tulo; koma Ine ndikupita kumeneko kukamudzutsa.”**

¹²Ophunzira ake anayankha kuti, “Ambuye, ngati wagona adzapeza bwino.” ¹³Yesu ankayankhula za imfa yake koma ophunzira ake ankaganiza kuti amanena za tulo chabe.

¹⁴Ndipo kenaka anawawuza momveka kuti, **“Lazaro wamwalira. ¹⁵Ine ndikukondwera chifukwa cha inu kuti kunalibe kumeneko; koma kuti mukakhulupirire tiyeni tipiteko.”**

¹⁶Pamenepo Tomasi, wotchedwa Didimo, anati kwa ophunzira anzake, “Tiyeni nafenso tipite, kuti tikaferere naye pamodzi.”

Yesu Atonthoza Alongo a Lazaro

¹⁷Yesu atafika, anapeza kuti Lazaro anali atagona m’manda masiku anayi. ¹⁸Mudzi wa Betaniya unali pafupi ndi Yerusalemu pa mtunda wosachepera makilomita atatu, ¹⁹ndipo Ayuda ambiri anabwera kwa Marita ndi Mariya kudzawatonthoza pa imfa ya m’bale wawo. ²⁰Pamene Marita anamva kuti Yesu akubwera, anapita kukakumana naye. Koma Mariya anatsala ku nyumba.

²¹Marita anati kwa Yesu, “Ambuye, mukanakhala muli kuno, mlongo wanga sakanamwalira. ²²Koma ine ndikudziwa kuti ngakhale tsopano Mulungu adzakupatsani chilichonse chimene mudzamupempha.”

²³Yesu anati kwa iye, **“Mlongo wako adzauka.”**

²⁴Marita anayankha kuti, “Ine ndikudziwa kuti adzauka pa kuukanso pa tsiku lomaliza.”

²⁵Yesu anati kwa iye, **“Ine ndine kuuka ndi moyo. Wokhulupirira Ine, angakhale amwalira adzakhala ndi moyo. ²⁶Aliyense amene ali ndi moyo ndi kukhulupirira Ine sadzamwalira. Kodi iwe ukhulupirira izi?”**

²⁷Marita anamuwuzira Iye kuti, “Inde Ambuye, ine ndikukhulupirira kuti ndinu Khristu, Mwana wa Mulungu, amene abwera m’dziko lapansi.”

²⁸Ndipo iye atanena izi anabwerera ndi kukayitana mchemwali wake Mariya namuyankhula monong’ona pambali, nati, “Aphunzitsi abwera ndipo akukuyitana.” ²⁹Mariya atamva izi, anayimirira mofulumira napita kwa Iye. ³⁰Tsopano n’kuti Yesu asanalowe m’budzi, koma anali akanali pa malo pamene Marita anakumana naye. ³¹Ayuda amene ankamutonthoza Mariya m’nyumba, anaona mmene iye anayimira mofulumira ndi kutuluka kunja, iwo anamutsata akuganzira kuti ankapita ku manda kukalirira kumeneko.

32Mariya anafika pamalo pamene panali Yesu ndipo atamuona, anagwa pa mapazi ake ndipo anati, “Ambuye mukanakhala muli kuno mlongo wanga sakanamwalira.”

33Yesu ataona iye akulira, ndi Ayuda amene anabwera naye akuliranso, anakhudzidwa kwambiri ndi kuvutika mu mzimu. 34Iye anafunsa kuti, “Kodi mwamuyika kuti?”

Iwo anayankha kuti, “Ambuye tiyeni mukaone.”

35Yesu analira.

36Pamenepo Ayuda anati, “Taonani mmene iye anamukondera Lazaro!”

37Koma ena a iwo anati, “Iye amatsekula maso a munthu wosaona, kodi sakanakhoza kuletsa kuti munthu uyu asamwalire?”

Yesu Aukitsa Lazaro

38Yesu atakhudzidwanso kwambiri anafika ku manda. Manda akewo anali phanga ndipo anatsekapo ndi mwala. 39Yesu anati, “**Chotsani mwala.**”

Marita mlongo wa womwalirayo anati, “Koma Ambuye, nthawi ino wayamba kununkha, pakuti wakhala m’menemu masiku anayi.”

40Kenaka Yesu anati, “**Kodi Ine sindinakuwuze kuti ngati iwe ukhulupirira, udzaona ulemerero wa Mulungu?**”

41Choncho iwo anachotsa mwalawo. Kenaka Yesu anayang’ana kumwamba ndikuti, “**Atate, Ine ndikukuthokozani chifukwa mumandimvera.** 42**Ine ndimadziwa kuti Inu mumandimvera nthawi zonse, koma Ine ndanena izi chifukwa cha anthu amene ayima pano, kuti iwo akhulupirire kuti Inu munandituma Ine.**”

43Yesu atanena izi, iye anayitana ndi mawu ofuwula kuti, “**Lazaro, tuluka!**” 44Munthu womwalirayo anatuluka, womangidwa miyendo ndi manja ndi nsalu za ku manda, ndi nkhope yake yokulungidwa nsalu.

Yesu anawawuza kuti, “**M’masuleni, ndipo muloleni apite.**”

Phunziro 24

CHIWOBOLO: Yesu aphunzitsa za wankulu mu ufumu wa Mulungu

Mateyu 20:20-28

Pempho la Mkazi wa Zebedayo

²⁰Amayi a ana a Zebedayo anabwera ndi ana ake kwa Yesu, nagwada pansu namupempha lye.

²¹Yesu anawafunsa kuti, **“Mukufuna chiyani?”**

Amayiwo anati, “Lolani kuti ana anga awiriwa adzakhale mmodzi ku dzanja lanu lamanja ndi wina ku dzanja lanu lamazere mu ufumu wanu.”

²²Yesu anawawuza kuti, **“Simukudziwa chimene mukupempha. Kodi mungathe kumwera chikho chimene ndidzamwera Ine?”**

Iwo anayankha nati, “Inde tingathe.”

²³Yesu anawawuza kuti, **“Zoonadi mudzamwera chikho changa, koma kuti mudzakhale ku dzanja langa lamanja kapena lamazere si kwa Ine kupereka. Malo awa ndi a iwo amene anakonzeredweratu ndi Atate anga.”**

²⁴Ophunzira khumi aja, anawapsera mtima abale awiriwo. ²⁵Yesu anawayitana onse pamodzi nati, **“Mukudziwa kuti olamulira a mitundu ina ali ndi mphamvu pa iwo, ndipo akuluakulu awo amawalamulira. ²⁶Siziyenera kutero ndi inu. M'malo mwake, aliyense amene akufuna kukhala wankulu pakati panu akhale wotumikira wanu. ²⁷Ndipo aliyense amene akufuna kukhala woyamba akhale kapolo wanu. ²⁸Momwenso Mwana wa Munthu sanabwere kudzatumikiridwa, koma kudzatumikira, ndi kupereka moyo wake kukhala dipo la anthu ambiri.”**

Phunziro 25

CHIWOBOLO: Mgonero wa Ambuye ndi kulosera za imfa ya Yesu

Mateyu 26:26-30

Chiwembu cha Ayuda pa Yesu

²⁶Pamene ankadya, Yesu anatenga buledi, nayamika ndipo anamunyema nagawira ophunzira ake nanena kuti, “Tengani, idyani; ili ndi thupi langa.”

²⁷Kenaka anatenga chikho, nayamika nachipereka kwa iwo nati, “Imwani nonsenu. ²⁸Awa ndi magari anga a pangano amene akhetsedwa chifukwa cha ambiri kuti akhululukidwe machimo. ²⁹Ndikuwuzani kuti sindidzamwanso kuchokera ku chipatso cha mtengo wa mpesa kuyambira lero mpaka tsiku ilo pamene ndidzamwanso mwatsopano ndi inu mu ufumu wa Atate anga.”

³⁰Atayimba nyimbo, anatuluka kupita ku phiri la Olivi.

Phunziro 26

CHIWOBOLO: Kupelekedwa ndi kuweluzidwa kwa Yesu

Yohane 18:1-40 19:16

Amugwira Yesu

¹Yesu atamaliza kupemphera, Iye anachoka ndi ophunzira ake ndi kuwoloka chigwa cha Kidroni. Kumbali inayo kunali munda wa Olivi, ndipo Iye ndi ophunzira ake analowamo.

²Tsopano Yudas, amene anamupereka amadziwa malowo chifukwa Yesu anakumana ndi ophunzira ake kumeneko. ³Choncho Yudas anabwera ku munda, akutsogolera gulu la asilikali ndi akuluakulu ena ochokera kwa akulu a ansembe ndi Afarisi. Iwo anali atanyamula miyuni, nyale ndi zida.

⁴Yesu, podziwa zonse zimene zimati zichitike kwa Iye, anatuluka ndi kuwafunsa kuti, **“Kodi mukufuna ndani?”**

⁵Iwo anayankha kuti, “Yesu wa ku Nazareti.”

Yesu anati, **“Ndine.”** (Ndipo Yudas womuperekayo anali atayima nawo pamenepo). ⁶Pamene Yesu anati, **“Ndine,”** iwo anabwerera m’mbuyo ndi kugwa pansu.

⁷Iye anawafunsanso kuti, **“Kodi mukumufuna ndani?”**

Ndipo iwo anati, “Yesu wa ku Nazareti.”

⁸Yesu anayankha kuti, **“Ine ndakuwuzani kuti Ndine. Ngati inu mukufuna Ine, asiye anthu awa apite.”** ⁹Izi zinachitika kuti mawu amene Iye anayankhula akwaniritsidwe: **“Ine sindinataye ndi mmodzi yemwe mwa iwo amene mwandipatsa.”**

¹⁰Kenaka Simoni amene anali ndi lupanga analitulutsa ndi kutema nalo wantchito wa wamkulu wa ansembe, nadula khutu lake la kudzanja lamanja. (Dzina la wantchitoyo ndi Makusi).

¹¹Yesu analamula Petro kuti, **“Bwezera lupanga m’chimake! Kodi Ine ndisamwere chikho chimene Atate andipatsa?”**

Amutengera Yesu kwa Anasi

¹²Kenaka gulu la asilikali ndi olamulira wawo ndi akuluakulu a Ayuda anamugwira Yesu. Iwo anamumanga. ¹³Poyamba anapita naye kwa Anasi amene anali mkamwini wa Kayafa, mkulu wa ansembe chaka chimenecho. ¹⁴Kayafa anali amene analangiza Ayuda kuti kukanakhala kwabwino ngati munthu mmodzi akanafera anthu.

Petro Akana Yesu Koyamba

¹⁵Simoni Petro ndi ophunzira wina ankamutsatira Yesu chifukwa ophunzira uyu amadziwika kwa mkulu wa ansembe. Iye analowa ndi Yesu m’bwalo la mkulu wa ansembe ¹⁶koma Petro anadikira kunjira pa khomo. Ophunzira winayo amene amadziwika kwa mkulu wa ansembe, anatuluka ndi kuyankhula ndi mtsikana amene anali mlonda wa pa khomo ndi kumulowetsa Petro.

¹⁷Mtsikanayo anafunsa Petro kuti, “Kodi iwe sindiwe mmodzi wa ophunzira a Munthu uyu?” Iye anayankha kuti, “Ayi, sindine.”

¹⁸Popeza kunkazizira, anyamata antchito ndi akuluakulu ena anasonkha moto wamakala namawotha atayimirira mozungulira. Petro nayenso anayimirira pamodzi ndi iwo namawotha nawo motowo.

Mkulu wa Ansembe Amufunsa Yesu

¹⁹Pa nthawi imeneyi, mkulu wa ansembe anamufunsa Yesu za ophunzira ake ndi chiphunzitsa chake.

²⁰Yesu anayankha kuti, **“Ine ndinayankhula poyera ku dziko lapansi. Nthawi zonse ndimaphunzitsa m’sunagoge kapena m’Nyumba ya Mulungu kumene Ayuda onse**

amasonkhana pamodzi. Ine sindimanena kanthu mseri. ²¹N'chifukwa chiyani mukundifunsa Ine? Afunsemi amene amamva. Zoonadi akudziwa zimene Ine ndinanena."

²²Yesu atanena izi, mmodzi wa akuluakulu amene anali pafupi anamumenya kumaso. Iye anafunsa kuti, "Mayankhidwe awa ndi woti ndi kuyankha mkulu wa ansembe?"

²³Yesu anayankha kuti, "Ngati Ine ndanena kanthu kolakwika, chitirani umboni chimene ndalakwa. Koma ngati ndanena zoonadi, n'chifukwa chiyani mwandimenya?" ²⁴Kenaka Anasi anamutumiza Iye, ali womangidwabe, kwa Kayafa, mkulu wa ansembe.

Petro Akana Yesu Kachiwiri ndi Kachitatu

²⁵Pamene Simoni Petro anali chiyimirire kuwotha moto, anafunsiwa kuti, "Kodi iwe si mmodzi wa ophunzira ake?"

Iye anayankha kuti, "Ayi, sindine."

²⁶Mmodzi wa antchito a mkulu wa ansembe, m'bale wa munthu amene anadulidwa khutu ndi Petro anamutsutsa iye kuti, "Kodi sindinakuone iwe pamodzi ndi Iye m'munda muja?" ²⁷Petro anakananso, ndipo pa nthawi yomweyo tambala analira.

Yesu ku Bwalo la Pilato

²⁸Kenaka Ayuda anamutenga Yesu kuchoka kwa Kayafa ndi kupita ku nyumba yaufumu ya bwanamkubwa wa Chiroma. Tsopano kunali mmamawa, ndipo polewa kudetsedwa monga mwa mwambo Ayuda sanalowe m'nyumba yaufumuyo; iwo anafuna kuti adye Paska. ²⁹Choncho Pilato anatuluka napita kwa iwo ndipo anati, "Kodi ndi milandu yanji imene mukumuzenga munthu uyu?"

³⁰Iwo anayankha kuti, "Ngati Iye akanakhala kuti si wolakwa, ife sitikanamupereka kwa inu."

³¹Pilato anati, "Mutengeni inu eni ake ndi kumuweruza Iye monga mwa malamulo anu."

Ayuda anatsutsa nati, "Koma tilibe ulamuliro wakupha aliyense." ³²Izi zinachitika kuti mawu a Yesu amene anayankhula kusonyeza mtundu wa imfa imene Iye anati adzafeyo nayo akwaniritsidwe.

³³Kenaka Pilato anapita m'kati mwa nyumba yaufumu nayitanitsa Yesu, ndipo anamufunsa kuti, "Kodi iwe ndi mfumu ya Ayuda?"

³⁴Yesu anafunsa kuti, "Kodi amenewo ndi maganizo anu wokha? Kapena kuti ena anakuwuzani za Ine?"

³⁵Pilato anayankha kuti, "Kodi iwe ukuganiza kuti ine ndine Myuda? Ndi anthu ako ndi akulu a ansembe ako amene akupereka iwe kwa ine. Kodi walakwanji?"

³⁶Yesu anati, "Ufumu wanga si wa dziko lapansi lino. Ukanakhala wa pansu pano, antchito anga akanachita nkondo kulepheretsa Ayuda kundigwira. Koma tsopano ufumu wanga ndi wochokera kumalo ena."

³⁷Pilato anati, "Kani ndiwe mfumu!"

Yesu anayankha kuti, "Inu mwalondola ponena kuti, Ine ndine mfumu. Kunena zoonadi, Ine ndinabadwa chifukwa cha chimenechi, ndipo n'chifukwa chake ndinabwera m'dziko lapansi, kudzachitira umboni choonadi. Aliyense amene ali mbali yachoonadi amamvera mawu anga."

³⁸Pilato anafunsa kuti, "Kodi choonadi n'chiyani?" Ndi mawu awa iye anapitanso kwa Ayuda ndipo anati, "Ine sindikupeza mandu mwa Iye. ³⁹Koma ndi mwambo wanu kuti pa nthawi ya Paska, ine ndikumasilireni wam'ndende mmodzi. Kodi mufuna ndikumasilireni 'Mfumu ya Ayuda?' "

⁴⁰Iwo anafuwula nati, "Ameneyu ayi! Mutipatse ife Baraba!" Barabayo anali wachifwamba.

Yesu Aweruzidwa kuti Aphedwe

¹Kenaka Pilato anatenga Yesu namukwapula mwankhanza. ²Asilikali analuka nkhatu yaminga ndi kumuveka pamutu pake. Kenaka anamuveka mkanjo wapepo ³ndipo ankapita kwa Iye mobwerezabwereza ndi kumanena kuti, "Moni mfumu ya Ayuda?" Ndipo amamumenya makofi.

⁴Pilato anatulukanso ndipo anati kwa Ayuda, “Taonani, ine ndikumubweretsa kuti inu mudziwe kuti ine sindikupeza chifukwa chomuyimbira mlandu.” ⁵Pamenepo Yesu anatuluka atavala nkhatu yaminga ndi mkanjo wapepo ndipo Pilato anawawuza kuti, “Nayu munthu uja!”

⁶Atangomuona iye akulu a ansembe ndi akuluakulu ena anafuwula kuti, “Mpachikeni! Mpachikeni!”

Koma Pilato anayankha kuti, “Inu mutengeni ndi kumupachika. Koma ine sindikupeza chifukwa chomuyimbira mlandu.”

⁷Ayuda anayimirira nati, “Ife tili ndi lamulo, ndipo molingana ndi lamulolo, iyeyu ayenera kuphedwa chifukwa akudzitcha kuti ndi Mwana wa Mulungu.”

⁸Pilato atamva zimenezi, anachita mantha kwambiri, ⁹ndipo anabwereranso m’nyumba yaufumu. Iye anafunsa Yesu kuti, “Kodi umachokera kuti?” Koma Yesu sanayankhe. ¹⁰Pilato anati, “Kodi ukukana kundiyankhula ine? Kodi sukuzindikira kuti ine ndili ndi mphamvu yokumasula ndiponso mphamvu yokupachika?”

¹¹Yesu anayankha kuti, “**Inu simukanakhala ndi mphamvu pa Ine akanapanda kukupatsani kumwamba. N’chifukwa chake amene wandipereka Ine kwa inu ndiye wochimwa kwambiri.**”

¹²Kuyambira pamenepo Pilato anayesa kuti amumasule Yesu, koma Ayuda anapitirira kufuwula kuti, “Ngati mumumasula munthuyu kuti apite, inu si bwenzi la Kaisara.”

¹³Pilato atamva zimenezi, iye anamutulutsa Yesu kunjani ndi kukhala pansu pa mpando wa woweruza pamalo otchedwa Mwala Wowaka (umene pa Chiaramaiki ndi Gabata). ¹⁴Linali tsiku lokonzekera Sabata la Paska ndipo nthawi inali ora lachisanu ndi chimodzi masana.

Pilato anati kwa Ayuda, “Nayi mfumu yanu.”

¹⁵Koma iwo anafuwula kuti, “Choka nayeni! Choka nayeni! Mpachikeni!”

Pilato anafunsa kuti, “Kodi ine ndipachike mfumu yanuyi?”

Akulu a ansembe anayankha kuti, “Ife tilibe mfumu ina koma Kaisara.”

¹⁶Pomaliza Pilato anamupereka kwa iwo kuti akapachikidwe. Choncho asilikali anamutenga Yesu.

Phunziro 27

CHIWOBOLO: *Yesu apachikidwa pa mtanda

Luka 23:32-56

³²Amuna ena awiri, onsewo achifwamba, anatengedwanso pamodzi ndi Yesu kukaphedwa. ³³Pamene anafika pamalo otchedwa Bade, anamupachika lye pamodzi ndi achifwambawo, mmodzi kudzanja lake lamanja ndi winayo la ku lamazere. ³⁴Yesu anati, “Atate, akhululukireni, pakuti sakudziwa chimene akuchita.” Ndipo anagawana malaya ake mochita maere.

³⁵Anthu anayimirira n’kumaonerera, ngakhale akuluakulu ankamulalatira lye. Iwo anati, “Iye anapulumutsa ena; adzipulumutse yekha ngati ndi Khristu wa Mulungu, Wosankhidwayo.”

³⁶Asilikalinso anabwera ndi kumunyoza lye. Iwo anamupatsa vinyo wosasa, ³⁷ndipo anati, “Ngati ndiwe Mfumu ya Ayuda, dzipulumutse wekha.”

³⁸Ndipo panalembedwa chikwangwani pamwamba pake chimene chinati: UYU NDI MFUMU YA AYUDA.

³⁹Mmodzi wa achifwambawo, amene anapachikidwa, anamunenera lye zamwano nati, “Kodi sindiwe Khristu? Dzipulumutse wekha ndi ifenso!”

⁴⁰Koma wachifwamba winayo anamudzudzula iye nati, “Suopa Mulungu, iwenso ukulandira chilango chomwechi? ⁴¹Ife tikulangidwa mwachilungamo, pakuti ife tikulandira monga mwa ntchito zathu. Koma munthu uyu sanachimwe kanthu.”

⁴²Kenaka anati, “Yesu, mundikumbukire ine pamene mulowa mu ufumu wanu.”

⁴³Yesu anayankha kuti, “Zoonadi, ndikukuwuzza kuti lero lino udzakhala ndi Ine m’paradaiso.”

Imfa ya Yesu

⁴⁴Linali tsopano pafupi ora lachisanu ndi chimodzi, ndipo mdima unagwa pa dziko lonse mpaka ora lachisanu ndi chinayi, ⁴⁵pakuti dzuwa linaleka kuwala. Ndipo chinsalu cha m’Nyumba ya Mulungu chinang’ambika pakati. ⁴⁶Yesu anafuwula ndi mawu okweza kuti, “Atate, ndikupereka mzimu wanga m’manja mwanu.” Atanena zimenezi, anamwalira.

⁴⁷Kenturiyo, ataona zimene zinachitikazi, analemekeza Mulungu ndipo anati, “Zoonadi, uyu anali munthu wolungama.” ⁴⁸Anthu onse amene anasonkhana kudzaonerera izi, ataona zinachitikazo, anadziguguda pachifuwa ndipo anachoka. ⁴⁹Koma onse amene anamudziwa lye, kuphatikiza amayi amene anamutsatira kuchokera ku Galileya, anayimirira akuona zinthu izi.

Yesu Ayikidwa M’manda

⁵⁰Ndipo taonani panali munthu wina wotchedwa Yosefe, mmodzi wa gulu loweruza, munthu wabwino ndi wolungama. ⁵¹Iye sanavomereze zimene anzake abwalo anagwirizana ndi kuchita. Iye ankachokera ku mudzi wa Arimateyu wa ku Yudeya ndipo ankayembekezera ufumu wa Mulungu. ⁵²Atapita kwa Pilato, iye anakapempha mtembo wa Yesu. ⁵³Ndipo anawutsitsa, nawukulunga nsalu yabafuta nawuyika m’manda wosemedwa m’mwala, amene panalibe wina amene anayikidwamo. ⁵⁴Linali tsiku lokonzekera ndipo Sabata linatsala pang’ono kuyamba.

⁵⁵Amayi amene anabwera ndi Yesu kuchokera ku Galileya, anatsata Yosefe ndipo anaona manda ndi momwe mtembo wake anawuyikira. ⁵⁶Kenaka anapita ku mudzi ndi kukakonza mafuta onunkhira. Koma anapuma pa tsiku la Sabata pomvera malamulo.

Phunziro 28

CHIWOBOLO: Yesu agonjetsa imfa

Luka 24:1-35

Yesu Auka kwa Akufa

¹Pa tsiku loyamba la Sabata, mmamawa kwambiri, amayi anatenga zonunkhira napita ku manda. ²Anaona mwala wa pa manda utagubuduzika ³ndipo atalowamo sanapeze mtembo wa Ambuye Yesu. ⁴Pamene iwo ankadabwa za zimenezi, mwadzidzidzi, amuna awiri ovala zovala zonyezimira kwambiri anayimirira pambali pawo. ⁵Ndi mantha, amayiwo anaweramitsa nkhope zawo pansu, koma amunawo anawawuza kuti, “N’chifukwa chiyani mukufuna wamoyo pakati pa akufa? ⁶Iye sali muno ayi. Wauka! Kumbukirani zimene anakuwuzani pamene anali nanu ku Galileya: ⁷‘**Mwana wa Munthu ayenera kuperekedwa m’manja mwa anthu ochimwa, napachikidwa ndipo tsiku lachitatu adzaukitsidwanso.**’” ⁸Ndipo anakumbukira mawu ake.

⁹Atabwerera kuchokera ku mandako, anafotokoza zinthu zonse kwa khumi ndi mmodziwo ndi kwa ena onse. ¹⁰Amayi anali Mariya Magadalena, Yohana, Mariya amayi a Yakobo, ndi ena anali nawo amene anawuza atumwi. ¹¹Koma iwo sanawakhulupirire amayiwa, chifukwa mawu awo amaoneka kwa iwo ngati opanda nzeru. ¹²Komabe Petro anayimirira ndi kuthamangira ku manda. Atasuzumira, anaona nsalu zimene anamukulungira zija zili pa zokha, ndipo iye anachoka, akudabwa ndi zimene zinachitikazo.

Zochitika pa Njira ya ku Emau

¹³Ndipo tsiku lomwelo, awiri a iwo ankapita ku mudzi wotchedwa Emau, pafupifupi makilomita khumi ndi imodzi kuchokera ku Yerusalemu. ¹⁴Iwo ankayankhulana za zonse zimene zinachitikazo. ¹⁵Pamenepo Yesu mwini wake anabwera ndi kuyenda nawo pamodzi; ¹⁶koma iwo sanamuzindikire.

¹⁷Iye anawafunsa kuti, “**Kodi mukukambirana zotani m’njira muno?**”

Iwo anayima ndi nkhope zakugwa. ¹⁸Mmodzi wa iwo wotchedwa Kaliyopa anamufunsa kuti, “Kodi ndiwe wekha wokhala mu Yerusalemu amene sukudziwa zinthu zimene zachitika m’masiku awa?”

¹⁹Iye anafunsa kuti, “**Zinthu zotani?**”

Iwo anayankha nati, “Za Yesu wa ku Nazareti, Iye anali mneneri, wamphamvu m’mawu ndi mu zochita pamaso pa Mulungu ndi anthu onse. ²⁰Akulu a ansembe ndi oweruza anamupereka Iye kuti aphedwe, ndipo anamupachika Iye; ²¹koma ife tinkayembekezera kuti Iye ndiye amene akanawombola Israeli. Ndipo kuwonjeza apo, lero ndi tsiku lachitatu chichitikireni izi. ²²Kuwonjezanso apo, ena mwa amayi athu atidabwitsa ife. Iwo anapita ku manda mmamawa ²³koma sanakapeze mtembo wake. Iwo anabwera ndi kudzatiwuzwa ife kuti anaona masomphenya a angelo amene anati Yesu ali moyo. ²⁴Kenaka ena mwa anzathu anapita ku manda ndipo anakapeza monga momwe amayiwo ananenera, koma Iye sanamuone.”

²⁵Iye anawawuza kuti, “**Inu ndinu anthu opusa, osafuna kukhulupirira msanga zonse zimene aneneri ananena! ²⁶Kodi Khristu sanayenera kumva zowawa izi ndipo kenaka ndi kulowa mu ulemero wake?**” ²⁷Ndipo kuyambira ndi Mose ndi aneneri onse Iye anawafotokozerwa zimene zinalembedwa m’malemba wonse zokhudzana ndi Iye mwini.

²⁸Atayandikira mudzi omwe amapitako, Yesu anachita ngati akupitirira. ²⁹Koma iwo anamupempha Iye kwambiri kuti, “Mukhale ndi ife, popeza kwatsala pang’ono kuda, ndipo dzuwa lili pafupi kulowa.” Ndipo Iye anapita kukakhala nawo.

³⁰Iye ali pa tebulo pamodzi nawo, anatenga buledi ndipo anayamika, nanyema nayamba kuwagawira. ³¹Kenaka maso awo anatesekuka ndipo anamuzindikira Iye, ndipo anachoka pakati pawo. ³²Iwo anafunsana wina ndi mnzake kuti, “Kodi mitima yathu sinali kutentha m’kati mwathu pamene Iye ankayankhulana naye pa njira ndi mmene anatitsekulira malemba?”

³³Nthawi yomweyo iwo anayimirira ndi kubwerera ku Yerusalemu. Iwo anapeza khumi ndi mmodziwo ndi ena anali nawo nasonkhana pamodzi ³⁴ndipo anati, “Ndi zoonadi! Ambuye auka

ndipo anaonekera kwa Simoni.”³⁵Kenaka awiriwo anawawuza zimene zinachitika pa njira, ndi mmene iwo anamudziwira Yesu, lye atanyema buledi.

Phunziro 29

CHIWOBOLO: Yesu azionetsera kwa ophunzira, nakwera kumwamba

Luka 24:36-53

Yesu Aonekera kwa Ophunzira

³⁶Akufotokoza zimenezi, Yesu mwini wake anayimirira pakati pawo ndipo anati, “Mukhale ndi mtendere.”

³⁷Koma chifukwa choti anathedwa nzeru ndi kuchita mantha, ankaganiza kuti akuona muzukwa. ³⁸Iye anawafunsa kuti, “N’chifukwa chiyani mukuvutika? N’chifukwa chiyani mukukayika mu mtima mwanu? ³⁹Taonani manja anga ndi mapazi anga. Ine ndine amene! Khudzeni kuti muone. Mzukwa ulibe mnofu ndi mafupa monga mukuonera ndili nazo.”

⁴⁰Iye atanena izi anawaonetsa manja ake ndi mapazi ake. ⁴¹Ndipo pamene iwo samakhulupirabe, chifukwa cha chimwemwe ndi kudabwa, Iye anawafunsa kuti, “Kodi muli ndi chakudya chilichonse pano?” ⁴²Iwo anamupatsa Iye kachidutswa ka nsomba yophika. ⁴³Iye anakatenga ndi kukadya iwo akuona.

⁴⁴Iye anawawuza kuti, “Izi ndi zimene ndinakuwuzani pamene ndinali nanu: chilichonse chiyenera kukwaniritsidwa chimene chinalembedwa cha Ine m’buku la Malamulo a Mose, Aneneri ndi Masalimo.”

⁴⁵Kenaka anawatsekula maganizo kuti azindikire Malemba. ⁴⁶Iye anawawuza kuti, “Izi ndi zimene zinalembedwa: Khristu adzazunzika ndipo adzauka kwa akufa tsiku lachitatu. ⁴⁷Ndipo kutembenuka mtima ndi kukhululukidwa kwa machimo zidzalalikidwa mu dzina lake kwa anthu amitundu yonse kuyambira mu Yerusalemu. ⁴⁸Inu ndinu mboni za zimenezi. ⁴⁹Ine ndidzakutumizirani chimene Atate anga analonjeza. Koma khalani mu mzinda muno mpaka mutavekedwa mphamvu yochokera kumwamba.”

Kupita Kumwamba

⁵⁰Iye atawatengera kunja kwa mzindawo mpaka ku Betaniya, anakweza manja ake ndi kuwadalitsa. ⁵¹Iye akuwadalitsa, anawasiya ndipo anatengedwa kupita kumwamba. ⁵²Pamenepo anamulambira Iye ndipo anabwerera ku Yerusalemu ndi chimwemwe chachikulu. ⁵³Ndipo iwo anakhalabe ku Nyumba ya Mulungu, akulemekeza Mulungu.

Phunziro 30

KUWOMBA NKOTA: Kodi mufuna kusatira mawu a Mulungu?

Yohane 3:1-21; Mateyu 7:13-14

Yesu Aphunzitsa Nekodimo za Kubadwa Kwatsopano

¹Ndipo panali Mfarisi wotchedwa Nekodimo, wa m'gulu lolamulira la Ayuda. ²Iye anabwera kwa Yesu usiku ndipo anati, “Rabi, ife tikudziwa kuti ndinu aphunzitsi wochokera kwa Mulungu, pakuti palibe amene angachite zizindikiro zodabwitsa zimene Inu mukuchita ngati Mulungu sali naye.”

³Poyankha Yesu ananena kuti, “Zoonadi, Ine ndikukuwuza kuti, ngati munthu sabadwanso mwatsopano sangathe kuona ufumu wa Mulungu.”

⁴Nekodimo anati, “Kodi munthu angabadwensho bwanji atakalamba? Kodi angalowe kachiwiri m'mimba ya amayi ake kuti abadwensho?”

⁵Yesu anayankha kuti, “Zoonadi, Ine ndikukuwuza kuti ngati munthu sabadwa mwa madzi ndi Mzimu Woyera, sangalowe mu ufumu wa Mulungu. ⁶Thupi limabereka thupi, koma Mzimu amabereka mzimu. ⁷Iwe usadabwe chifukwa ndakuwuza kuti, ‘Uyenera kubadwanso.’ ⁸Mphepo imawomba kulikonse kumene ikufuna. Ungathe kumva kuwomba kwake, koma sungathe kudziwa kumene ikuchokera kapena kumene ikupita. N'chimodzimodzi ndi amene abadwa ndi Mzimu Woyera.”

⁹Nekodimo anafunsa kuti, “Kodi izi zingatheke bwanji?”

¹⁰Yesu anati, “Iwe mphunzitsi wa Israeli, kodi sukuzindikira zimenezi? ¹¹Zoonadi, Ine ndikukuwuza kuti ife tiyankhula zimene tikuzidziwa ndi kuchitira umboni zimene taziona, komabe inu simuvomereza umboni wathu. ¹²Ine ndikuyankhula kwa iwe zinthu za dziko lapansi ndipo sukukulupirira. Nanga kodi udzakhulupirira bwanji ngati nditayankhula zinthu zakumwamba? ¹³Palibe wina aliyense anapita kumwamba, koma yekhayo amene watsika kuchokera kumwamba, Mwana wa Munthu. ¹⁴Tsono monga Mose anapachika njoka m'chipululu, moteronso Mwana wa Munthu ayenera kupachikidwa, ¹⁵kuti aliyense amene akhulupirira lye akhale ndi moyo wosatha.

¹⁶“Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi, kotero anapereka Mwana wake wobadwa yekha, kuti aliyense wokhulupirira lye asatayike koma akhale ndi moyo wosatha. ¹⁷Pakuti Mulungu sanatume Mwana wake ku dziko lapansi, kuti akaweruze, koma kuti akapulumulutse dziko lapansi. ¹⁸Aliyense wokhulupirira lye saweruzidwa, koma aliyense wosakhulupirira waweruzidwa kale chifukwa sanakhulupirire dzina la Mwana wobadwa yekha wa Mulungu. ¹⁹Ndipo chiweruzo ndi ichi: kuwunika kunabwera m'dziko lapansi, koma anthu anakonda mdima m'malo mwa kuwunikako, chifukwa ntchito zawo zinali zoyipa. ²⁰Aliyense wochita zoyipa amadana ndi kuwunika, ndipo sabwera poyera chifukwa cha mantha kuti ntchito zake zingaonekere. ²¹Koma aliyense wokhala mu choonadi amabwera ku kuwunika, kuti zionekere poyera zimene iye wachita zachitika kudzera mwa Mulungu.”

Zipata Ziwiri ndi Njira Ziwiri

¹³ “Lowani pa chipata chopapatiza. Pakuti chipata cholowera kuchiwonongeko n'chachikulu ndipo msewu wake ndi waukulunso. Ndipo anthu ambiri amalowera pamene. ¹⁴Koma chipata ndi chopapatiza ndi msewu ndi waung'ono umene utsogolera anthu ku moyo wosatha ndipo ndi owerengeka okha amene ayipeza njirayo.



<https://discoverapp.org/get>

Biblica® Tsekulani Mawu a Mulungu mu Chichewa Chalero™. Mwini © 2002, 2016 ndi Biblica, Inc. “Biblica” ndilo dzina lodziwika la ntchitoyi ku United States limene linalembetsedwa ndi Biblica mwini. Limagwiritsidwa ntchito ndi chilolezo.

Kuwala Baibulo App - discoverapp.org

Reproduced under a Creative Commons ShareAlike 4.0 License

v1.0 16 May 2024